
**IMBIRANI
YEHOVA
MOSANGALALA**

BUKU LA MAWU OKHA

IMBIRANI YEHOVA MOSANGALALA

—1 MBIRI 15:16

BUKU LA MAWU OKHA

Dzina

Mpingo

Bukuli sitigulitsa. Timapereka ngati njira imodzi yophunzitsira Baibulo padziko lonse ndipo ndalama zoyendetsera ntchitoyi ndi zimene anthu amapereka mwa kufuna kwawo.

Ngati mukufuna kupereka ndalama, pitani pawebusaiti yathu ya donate.jw.org.

*Imbirani Yehova Mosangalala—Buku la Mawu Okha
“Sing Out Joyfully” to Jehovah—Lyrics Only
Losindikizidwa mu March 2020*

Chichewa (sjjyls-CN)

© 2017

Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Ofalitsa

Watchtower Bible and Tract Society of
New York, Inc., Wallkill, New York, U.S.A.

Made in Japan

Lopangidwa ku Japan



sjjyls-CN
201124

Mlozera

| | |
|-----------------------------------|---------|
| <i>Yehova</i> | 1-12 |
| <i>Yesu/Dipo</i> | 13-20 |
| <i>Ufumu</i> | 21-24 |
| <i>Odzozedwa ndi Ankhosa Zina</i> | 25-27 |
| <i>Ubwenzi ndi Yehova</i> | 28-40 |
| <i>Pemphero</i> | 41-47 |
| <i>Kudzipereka</i> | 48-52 |
| <i>Utumiki Wathu</i> | 53-84 |
| <i>Kusonkhana Pamodzi</i> | 85-93 |
| <i>Malemba</i> | 94-98 |
| <i>Ubale Wathu</i> | 99-103 |
| <i>Makhalidwe a Mulungu</i> | 104-130 |
| <i>Banja/Mabwenzi</i> | 131-138 |
| <i>Chiyembekezo Chathu</i> | 139-147 |
| <i>Kupulumutsidwa/Kuukitsidwa</i> | 148-151 |

1

Makhalidwe a Yehova

(Chivumbulutso 4:11)

1. Yehova ndinu M'lungu wamphamvu,
Moyo, kuwala zichoka kwa inu.
Chilengedwe chanu chilengeza;
Za mphamvu zanu zazikulu.
2. Mumaweruza mwachilungamo.
Malamulo anu ndi olungama.
Tikamawerenga Mawu anu
Timaona nzeru zakuya.
3. Chikondi chanu ndi chachikulu.
Mumatipatsa mphatso zapamwamba.
Za dzina ndi makhalidwe anu,
Tilengeza mosangalala.

2

Dzina Lanu Ndinu Yehova

(Salimo 83:18)

1. Mulungu woona—
 Mlengi wa zinthu zonse
Mulungu wamuyaya—
 Ndinudi Yehova.
Ndifetu amwayi
 Kukhala anthu anu.
Tilengeza za inu,
 Ku mitundu yonse.

(KOLASI)

Yehova, Yehova,

M'lungu ndinu nokha.

Kumwambako ndi padziko

Palibenso wina.

Ndinudi Wamphamvuyonse

Onsetu adziwe.

Yehova, Yehova,

M'lungu wathu ndinu nokha.

2. Tingathe kukhala
Chilichonse mwafuna.
Tigwire ntchito yanu—
Ndinudi Yehova.
Mwatipatsa dzina
Tikhale Mboni zanu.
Uwu ndi mwayi wathu—
Tikutamandani.

(Kolasi)

3 Ndinu Mphamvu Zathu, Chiyembekezo Chathu Komanso Timakudalirani (Miyambo 14:26)

1. O, Yehova mwatiphunzitsa
za moyo wosatha.
Zimatikhudzadi mtima
n'kuphunzitsa ena.
Nthawi zina timada nkhawa
chifukwa cha mavuto.
Chiyembekezo chathunso
chimatha kuchepa.

(KOLASI)

*Inu Mulungu ndinu
mphamvu yathu.
Inde mumatithandiza.
Mwalimbitsa,
chiyembekezo chathu
timadalira inuyo.*

2. Yehova muzitikumbutsa
tisamaiwale,
Zoti mumatithandiza
kutumikirabe.
Tikakumbukira mfundoyi
sitimaopa kanthu.
Koma timalimba mtima
pophunzitsa anthu.

(Kolasi)

4 “Yehova Ndi M’busa Wanga”

(Salimo 23)

1. Yehova ndi M’busa wanga;
Adzanditsogolera.
Amadziwa zofuna zanga;
Zomwe ndifunikadi.
Andipititsa kumsipu,
Malo otetezeka.
Mwachikondi chakedi chosatha
Mtendere wandipatsa.
Mwachikondi chake chosatha
Mtendere wandipatsa.
2. Njira zanu ndi zabwino,
Zonse n’zachelungamo.
Zochita zanga nthawi zonse
Zikulemekezeni.
Poyenda m’zigwa za mdima,
Mumandilimbikitsa,
Sindidzaopatu chilichonse,
Chifukwa muli nane.
Sindidzaopa chilichonse,
Chifukwa muli nane.

3. M'lungu ndinu M'busa wanga;
Ndidzakutsatirani.
Mumandilimbikitsa zedi;
Zonse mumandipatsa.
Poti ndinudi wamoyo,
Ndimakudalirani.
Kukoma mtima kwanu kosatha
Muzindisonyezabe.
Kukoma mtimatu kosatha
Muzindisonyezabe.

5 *Ntchito Zodabwitsa za Mulungu* (Salimo 139)

1. M'lungu mumandidziwa bwino,
Ndikagona ndipo ndikadzuka.
Mumafufuza maganizo anga,
Mawu ndi njira zanganso
mumadziwa.

Munandiona ndili m'mimba,
Munaonanso mafupa anga.
Munalemba ziwalo zanga zonse.
M'lungu wamphamvu
ndidzakutamandani.

Nzeru zanu, Mulungu, n'zodabwitsa;
Zimenezi ndithu ndikudziwa.
Ndikaopa kupezedwa ndi mdima,
Mzimu wanu udzandipezabe.

N'kuti komwe ndingabisale,
Komwe inu simungandione?
Kumanda kodi kapena kumwamba
Mumdima, m'nyanja;
ayi ndithu kulibe.

6 *Kumwamba Kumalengeza Ulemelero wa Mulungu* (Salimo 19)

1. Kumwamba kumatamanda Yehova.

Ntchito zake zonse
ndi zoonekera.

Tsiku ndi tsiku zimam'tamanda.

Nyenyenzi zimasonyeza,
kuti ndi wamphamvu.

2. Malamulo a M'lungu ndi angwiro,

Mawu ake onse
amatiteteza.

Amaweruzanso molungama.

Mawu ake ndi oona,
N'ngoyera, n'ngokoma.

3. Tidzaopa Mulungu kwamuyaya.

Malamulo ake
aposa golide.

Iwotu amatitsogolera.

Dzina lake loyeralo
Tililemekeze.

7 Yehova Ndiye Mphamvu Zathu

(Yesaya 12:2)

1. Yehova inu ndi mphamvu yathu,
Inu ndinu Mpulumutsi wathu.
Ndife Mboni za uthenga wanu,
Ngakhale anthu azitinyoza.

(KOLASI)

*Yehova, thanthwe ndi mphamvu zathu,
Tilengezabe dzina lanu.
Yehova inu wamphamvuyonse,
Pobisala pathu nsanja yathu.*

2. Kuwala kwanu n'kosangalatsa;
Maso athu aona cho'nadi.
Malamulo anu tawadziwa,
Tidzasankhatu Ufumu wanu.

(Kolasi)

3. Chifuniro chanu tichitabe.
Ngakhale Satana 'matinyoza.
Kaya atiphe tithandizeni
Kukhala kumbali yanu M'lungu.

(Kolasi)

8 *Yehova Ndiye Pothawirapo Pathu* (Salimo 91)

1. Yehova m'pothawira,
Timamudalira.
Tikhalebe mumthunzi;
Wake tisachoke.
Iye adzatiteteza,
Tikhulupirire ndithu.
Yehova m'phamvu zathu,
Ateteza olungama.
2. Kaya ambiri agwe
Pafupi ndi ife,
Yehova satisiya
Adzatiteteza.
Choncho tisachite mantha;
Tsoka silidzatigwera.
Yehova M'lungu wathu,
Adzatibisa m'mapiko.
3. Ku misampha yambiri
Adzatiteteza,
Zoopsa zilizonse,
Sitidzaziopa.
Zoopsa zonse zidzatha
Kulikonse tidzapita.
Yehova m'pothawira,
Adzatiteteza ndithu.

9 *Yehova Ndi Mfumu Yathu* (Salimo 97:1)

1. Kondwa lemekeza Yehova,
Kumwamba kulengeza chilungamo.
Mosangalala tiimbire Mulungu,
Tiuze onse ntchito zake.

(KOLASI)

*Kumwamba kukondwe, Dziko likondwere,
Chifukwa Yehova ndi Mfumu.
Kumwamba kukondwe, Dziko likondwere,
Chifukwa Yehova ndi Mfumu.*

2. Nena za kukwezeka kwake,
Chifukwa ndiye wotipulumutsa.
Yehova, tiyenera kumutamanda.
Tiyenitu timugwadire.

(Kolasi)

3. Wakhazikitsatu Ufumu.
Waika Mwana wake pampanowo.
Milungu yabodza
ichite manyazi,
Titamande Yehova yekha.

(Kolasi)

10 Tamandani Yehova Mulungu Wathu

(Salimo 145:12)

1. Tamanda Yehova M'lungu!
Dzina lakelo lengeza.
Chenjeza! Anthu adziwe,
Tsiku lake layandikira.
Walamula kuti Mwana wake,
Akhale Mfumu padziko.
Kauzeni anthu uthengawu,
Ndi madalitso akenso!

(KOLASI)

Tamanda Yehova M'lungu!
Lengeza kuti ndi wamkulu!

2. Tamanda, Imba mokweza!
Mosangalala Imbani!
Ndi mtima, woyamikira
Tilengeza ulemerero.
Ngakhale Mulungu ndi wamkulu,
Koma amadzichepetsa.
Ndi wachifundo chachikuludi;
Amayankha mapemphero.

(Kolasi)

11 Chilengedwe Chimatamanda Mulungu (Salimo 19)

1. Yehova ntchito zanu n'zambiri,
Zakumwamba zitamanda inu.
Chilengedwe chinena za inu;
Ngakhale sichitulutsa mawu.
Chilengedwe chinena za inu;
Ngakhale sichitulutsa mawu.
2. Nzeru yeniyeni ndi yabwino,
Imateteza okuopani.
Mfundo zanu zoposa golide—
N'zothandiza ana ndi akulu.
Mfundo zanu zoposa golide—
N'zothandiza ana ndi akulu.
3. Kudziwa inu n'kothandizadi,
Mawu anu, amapatsa moyo.
Oyeretsa dzina lanu onse,
Mudzawapatsatu madalitso.
Oyeretsa dzina lanu onse,
Mudzawapatsatu madalitso.

12 *Yehova Ndi Mulungu Wamkulu* (Ekisodo 34:6, 7)

1. Inu Yehova, M'lungu Wamkulu,
Wabwino m'zinthu zonse,
Tidzakutamandani.
Muli ndi mphamvu, chikondi, nzeru.
Mulungu wathu ndinu.
2. Timaonanso chifundo chanu.
Ngakhale ndife fumbi,
Tikapempha mumamva.
Mumatidyetsa, kutiphunzitsa,
Mumatithandizadi.
3. Tikutamanda inu Yehova.
Tikukuimbirani
Mosangalala ndithu.
Muyeneradi kutamandidwa.
Kuchokera mumtima.

13 *Khristu Ndi Chitsanzo Chathu* (1 Petulo 2:21)

1. Yehova Mulungu,
Anatikondadi,
Potipatsa dipo la Mwana wake.
Khristu anakhala—
Ngati anthu tonse—
Ndipo analemekeza M'lungu.
2. Mawu a Yehova,
Anati n'chakudya.
Chimene chinamupatsadi nzeru.
Anatumikira,
Mofunitsitsadi;
Ndipo anasangalatsa M'lungu.
3. Titsanzire Yesu
Potamanda M'lungu,
Komanso muzochita zathu zonse.
M'moyo wathu wonse
Titsanzire Yesu,
Ndipo tidzasangalatsa M'lungu.

14 *Tamandani Mfumu Yatsopano Yolamulira Dziko Lapansi* (Salimo 2:12)

1. Khamu lochokera m'mitundu
yonse lasonkhana,
Khristu ndi odzozedwa
akulisonkhanitsatu.
Ufumu wa Mulungu wabadwa;
Tipempha ubwere.
Chiyembekezochi ndi mphatso,
Chimatisangalatsadi.

(KOLASI)

*Tamandani M'lungu; Tamandani Yesu—
Iye ndi Mfumu ya mafumu.
Mogwirizana timvera Yesu
Ndiponso tim'tamanda.*

2. Titamande Mfumu yathu poimba,
mwachimwemwe.
Kalonga Wamtendereyu
adzatipulumutsa.
Tidzasangalala kukhala
M'dziko mopanda mantha,
Akufa adzawaukitsa.
Tonse tidzasangalala.

(Kolasi)

15 *Tamandani Mwana Woyamba Kubadwa wa Yehova* (Aheberi 1:6)

1. Tamandani Yesu,
Mfumu yodzozedwayo.
Yokonda choonadi;
Komanso chilungamo.

Popereka ulemu
Ku dzina la M'lungu,
Ulamuliro wake,
Adzalengezatu.

(KOLASI)

*Tamandani Yesu!
Wodzozedwa wa M'lungu.
Wakhala pa Ziyoni,
Mongatu Mfumu yathu!*

2. Tamandani Yesu,
Yemwe anatifera.
Anapereka dipo;
Timakhululukidwa.

Mkwatibwi wake pano
Akudikirira.
Ukwati n'ngwakumwamba
Udzakweza M'lungu.

(Kolasi)

16 *Tamandani Yehova Chifukwa cha Mwana Wake Wodzozedwa* (Chivumbulutso 21:2)

1. Yehova 'nadzoza Yesu
Kuti alamulire.
Kuti chifuniro cha M'lungu,
Padzikoli chichitike.

(KOLASI)

*Tamandani Yehova M'lungu,
Chifukwa cha wodzozedwa.
Inu nkhosa zokhulupirika
Zomvera malamulo.
Tamandani wodzozedwayo,
Wolamula wakumwamba,
Amene adzayeretsa dzina
Loyera la Mulungu.*

2. Abale a Yesu Khristu.
M'lungu amawasankha.
Adzalamulira ndi Yesu
Dzikoli adzayeretsa.

(Kolasi)

1. Khristu anasonyezatu,
Chikondi, kukoma mtima.
Pobwera padziko,
n’kutithandiza
M’mawu komanso zochita;
Ankakonda ovutika
Anachiritsa odwala.
Ndi kukwaniritsa ntchito yake
Ananena: “Ndikufuna.”
2. Tifuna kumutsanzira
M’zonse zomwe timachita.
Timasonyezatu
kukoma mtima,
Pophunzitsa ’nthu kumvera.
Anzathu akavutika;
Tiwasonyeze chikondi.
Choncho amasiye akapempha.
Tidzanena: “Ndikufuna.”

18 *Tikuthokoza Chifukwa cha Dipo*

(Luka 22:20)

1. Lero tabweratu,
kwa inu Yehova,
Chifukwa munatisonyezadi
chikondi.
Munapereka Mwana,
wanu woyamba.
Monga nsembe yoposa ina
iliyonse.

(KOLASI)

*Anafera anthu onse.
Kuti tidzapulumuke.
Tikuthokoza ndi mtima wonse,
Inu M'lungu.*

2. Mofunitsitsa Yesu
anapereka.
Nsembe ya dipo moti
tikusangalala.
Asanabwere
kudzatipulumutsa.
Sitinkayembekezera,
moyo wosatha.

(Kolasi)

19 Chakudya Chamadzulo cha Ambuye

(Mateyu 26:26-30)

1. Yehova 'Tate wakumwamba,
 Usikuwu n'ngwapadera.
Kale patsikuli munasonyezatu
 Chikondi, nzeru ndi mphamvu.
Mwana wankhosa anaphedwa,
 Anthu anamasulidwa.
Kenako Yesu anakhetsa magazi
 Kukwaniritsa ulosiwu.
2. Mkate ndi vinyo n'zokumbutsa,
 Kufunika kwa nsembeyi.
Komanso mphatso
 yomwe munatipatsa,
 Mwana wanu wokondedwa.
Madzulo ano tiyenera,
 Kuchita chikumbutsochi
Pokumbukira
 zomwe zinachitika
 Kuti dipo liperekedwe.

3. Tasonkhana pamaso panu.
Tamva kuitana kwanu
Titamande inu
ndi Mwana wanunso
Munatikonda kwambiri.
Mwambo wokulemekezani
Umatilimbikitsanso.
Tiyendebe motsatira Yesu Khristu,
Ndipo tidzapezadi moyo.

20

Munapereka Mwana Wanu Wobadwa Yekha

(1 Yohane 4:9)

1. Yehova, tinali
 opanda tsogolo.
Komano dipo
 lathandiza tonse.
Tikudzipereka,
 kwa inu kosatha.
Tiphunzitse ena,
 Akudziweninso.

(KOLASI)

*Mwana wanu yekha,
 munamupereka.
Tidzakuimbirani,
 za mphatsoyi kwamuyaya.*

2. Chifundo chanucho
ndi chachikuludi.
Komanso timakonda
dzina lanu.
Yoposa zonsezi,
ndi mphatso ya Yesu.
Anatifera kuti
tipulumuke.

(Kolasi)

(KUMALIZA)

Yehova, Atate, tikuthokozatu.
Mphatsoyi munatipatsadi kwamuyaya.

*Pitirizani Kufunafuna
Ufumu Choyamba*
(Mateyu 6:33)

1. Chofunika kwa Yehova,
Chomwe chim'sangalatsa,
Ndicho Ufumu wa Khristu,
Womwe ukonze zonse.

(KOLASI)

*M'fune Ufumu choyamba
Ndi chilungamo chake.
M'tamandeni mumitundu,
Ndi kum'tumikirabe.*

2. Musade nkhawa n'zamawa,
Za chakudya ndi madzi
M'lungu adzatipatsatu
Tikafuna Ufumu.

(Kolasi)

3. Choncho muzilalikira;
Muzithandiza ena
Kudaliranso Yehova
Ndi Ufumu wakenso.

(Kolasi)

Ufumu Umene Ukulamulira Kumwamba Ubwere

(Chivumbulutso 11:15; 12:10)

1. Yehova Mulungu wathu,
Ndinu wamuyaya.
Mwapatsa Yesu Ufumu,
Mwa kufuna kwanu.
Ufumu udzalamula
Padziko lonse lapansi.

(KOLASI)

Zafika tsopano

Ufumu chipulumutso.

Ufumu wayamba.

Tipempha kuti: “Ubwere!”

2. Nthawi ya Satana yatha;
Dziko latsopano
Lili pafupi kwambiri.
Mavuto adzatha.
Ufumu udzalamula
Padziko lonse lapansi.

(Kolasi)

3. Angelo asangalala,
Aimba mokondwa.
Satana wachotsedwako,
Onse akondwera.
Ufumu udzalamula;
Padziko lonse lapansi.

(Kolasi)

23 Yehova Wayamba Kulamulira

(Chivumbulutso 11:15)

1. Ufumu wa Mulungu.

Wayamba kulamula.

Khristu ndiye mwala mu Ziyoni.

Tonse tikweze mawu.

Tiimbire Mulungu.

Khristu Mpulumutsi,
wakhala pampando.

(KOLASI)

Ufumu ubweretsa chani?

Choonadi n'chilungamo.

Udzabweretsanso chiyani?

Moyo wosatha n'chimwemwe.

Tamanda Mfumu yosatha

Iye ndi wachikondi.

2. Khristu ali pampando,

Amagedo yafika.

Dongosolo la Satana litha.

Choncho tilalikire.

Ambiri amve mawu;

Ofatsa onse abwere

kwa Mulungu.

(Kolasi)

3. Tilemekeza Mfumu.

Yomwe ndi yodabwitsa.

Ikubwera m'dzina la Mulungu.

Lowani pachipata;

M'lungu mum'pembedzere.

Posachedwa

adzalamulira dziko.

(Kolasi)

24 *Bwerani Kuphiri la Yehova* (Yesaya 2:2-4)

1. Phiri la Yehova,
Tangoliyang'anani.
Latalika kuposa
Ena onse lero.

Anthu akubwera,
Kuchokera kutali,
Akuitanizana,
'Bwerani kwa M'lungu.'

Tsopano wamng'ono
Wakhala mtundu waukulu,
Tikuona kuti,
Tikudalitsidwa ndi M'lungu.

Ambiri tsopano
Akuvomerezadi.
Ulamuliro wake
Mokhulupirika.

2. Yesu walamula

Kuti tipite ndithu.

Tikalalikire

Uthenga wa Ufumu.

Khristu wayambano

Ulamuliro wake.

Iye akuti tikhale

Kumbali yake.

Ndi zosangalatsa,

Kuona khamu lalikulu.

Likukulirabe,

Ndipo tonse tikuthandiza.

Tonse tifuule,

Tiitanetu anthu,

‘Bwerani kuphiri

la Yehova Mulungu.’

1. Odzozedwa ndi mtundu,
Watsopano wa M'lungu.
Iye anawagula,
Padziko lapansi.

(KOLASI)

*N'chuma chapadera,
Otchedwa dzina lanu
Amakukondani.
Amalengezadi za inu.*

2. Ndi mtundu woyeradi,
Wophunzitsa cho'nadi.
Mulungu wawapatsa
Kuwala kwakedi.

(Kolasi)

3. Amasonkhanitsanso,
Nkhosa zina mwakhama.
Ndi okhulupirika.
Kwa Mwanawankhosa.

(Kolasi)

1. Nkhosa zina zomwe Yesu ali nazo,
zimatumikira ndi odzozedwa.
Zomwe nkhoa zina
zingawachitire
Yesu adzawabwezeratu zonse.

(KOLASI)

*“Mwakuwatonthoza, mwanditonthoza.
Zonse zimene munawachitira
munachitiranso ine amene.
Zonse zomwe munawachitira.
Munachitiranso ine amene.”*

2. “Pamene ndinali wanjala, waludzu,
munandithandiza mwamsanga ndithu.”
“Mbuye, tinachita
liti zimenezi?”
Ndiyeno Mfumu idzayankha kuti:

(Kolasi)

3. “Mwakhulupirika pochita zabwino,
polalikira ndi abale anga.”
Choncho Mfumuyo
idzauza nkhosazo:
“Landirani dziko, moyo wangwiro.”

(Kolasi)

27 Ulemerero wa Ana a Mulungu Udzaonekera (Aroma 8:19)

1. Posachedwa M'lungu wathu
Odzozedwa ake,
Adzawasonyeza kuti
ndi ana akedi.

(KOLASI)

*Khristu ndi odzozedwawo
Adzapambanadi.
Ulemerero wawonso
Udzaonekera.*

2. Posachedwa otsalira
Adzaitanidwa.
Khristu Mfumu ya mafumu,
adzatenga onse.

(Kolasi)

(VESI LOKOMETSER)

*Limodzi ndi Mbuye wawo
adzamenya nkondo.
Ukwati ndi Mbuye Yesu
Udzachitikatu.*

(Kolasi)

28 *Tikhale pa Ubwenzi ndi Yehova* (Salimo 15)

1. Ndani angakhale
 bwenzi lanu M'lungu?
 Ndani mungam'khulupirire,
 Angakhale mnzanu?
Ndani onse amene,
 Amakukondani,
 Amakukhulupirirani,
 Okonda cho'nadi.
2. Ndani angakhale
 bwenzi lanu M'lungu?
 Ndani angafike kumpando
 wanu wachifumu?
Ndani onse amene,
 Amakumverani,
 Olemekeza dzina lanu
 Okulambirani.
3. Timakuuzani,
 Zamumtima mwathu,
 Ndipo timamva
 Kuti tili pafupidi nanu.
Tifuna kukhala.
 Mabwenzi a inu.
 Palibiretu bwenzi,
 Lomwe lingakuposeni.

29 *Tizichita Zinthu Zogwirizana ndi Dzina Lathu*

(Yesaya 43:10-12)

1. Yehova, wamphamvuyonse wam'yaya,
Wamphamvu, chilungamo, n'chikondi.
Mwini choonadi komanso nzeru,
Mukulamulira monga Mfumu.
Timasangalala potumikira,
Ndi kulengeza Ufumu wanu.

(KOLASI)

*Ndi mwayidi kukhala Mboni zanu.
Tichite monga mwa dzina lathu.*

2. Tikamatumikira ndi abale
Timakhaladi ogwirizana.
Pophunzitsa anthu cho'nadi chanu,
Timakhalanso osangalala.
Timadziwikanso ndi dzina lanu,
Ndi mwayi wathu kulitchukitsa.

(Kolasi)

30 *Atate Wanga, Mulungu Wanga Ndiponso Bwenzi Langa* (Aheberi 6:10)

1. Nthawi zina m'dzikoli.
Moyo ungakhale wovuta.
Komabe ndizingoti,
'Moyo n'ngofunika.'

(KOLASI)

*M'lungu ndi wolungama,
chikondi changa saiwala.
Ali pafupi nane;
Nthawi zonse sanditaya.
Ndiye adzandipatsa
zonse zomwe ndifunikira.
Ndi Atate,
ndi Mulungu, Bwenzi langa.*

2. Unyamata wadutsa;
Tsopano ndi nthawi yovuta.
Koma chiyembekezo,
Changa ndi champhamvu.

(Kolasi)

1. Yendanitu ndi Mulungu;
Musonyeze chikondi.
Ndipo musachoke kwa Yehova,
Akulimbitsenitu.
Mawu akewo muzisunga;
Simudzasochera.
Muzimveratu Mulungu
Akutsogolereni.
2. Yendanitu mu chiyero;
Muzipewa zoipa.
Mayesero angakule bwanji,
Mudzawapiriratu.
Zinthu zonse zotamandika
Ndiponso zooni,
N'zomwe muziganizira,
M'lungu sakusiyani.
3. Yendanitu ndi Mulungu;
Mudzasangalaladi.
Zabwino zomwe amapereka
Muzimuthokozatu.
Yendanibe ndi M'lungu wathu;
Muzimuimbira.
Chimwemwecho ndi umboni,
Woti ndinu a M'lungu.

32 *Khalani Okhulupirika kwa Yehova* (Ekisodo 32:26)

1. Kale tinalitu achisoni,
Tinali m'chipembedzo chonyenga;
Koma tinasangalala zedi
Titamva za Ufumu.

(KOLASI)

*Yenda ndi Yehova; Usangalale.
Sangakusiyetu; Yenda m'kuwala.
Lengeza uthenga Wamtenderewu.
Ufumu wa Khristu Sudzatha konse.*

2. Timayenda naye nthawi zonse,
Polalikira kwa anthu onse.
Pano anthu adzisankhiretu,
Kumvera M'lungu wathu.

(Kolasi)

3. Mdyerekezi Sitidzamuopa.
Tidzakhulupirira Yehova.
Kaya adani angachuluke,
M'lungu ndi mphamvu yathu.

(Kolasi)

33 *Umutulire Yehova Nkhawa Zako* (Salimo 55)

1. Chonde ndimveni Yehova,
Musandinyalanyaze.
Imvani ululu wanga;
Chonde mundithandize.

(KOLASI)

*Tulira Yehova nkhawa;
Iye adzakupulumutsa.
Amateteza ndipo ndi
wokhulupirikanso.*

2. N'kanakhala ndi mapiko,
Ndikanaulukadi,
Kuti ndibisale,
ondichitira zoipawo.

(Kolasi)

3. M'lungu akatitonthoza,
Timapeza mtendere.
Adzatithandiza kuti
tipirire mavuto.

(Kolasi)

34 *Kuyenda ndi Mtima Wosagawanika* (Salimo 26)

1. Mundiweruzetu Mbuye wanga;
Onani kuti ndimakudalirani.
Ndifufuzeni ndi kundiyesa;
Konzani mtima wanga, mundidalitse.

(KOLASI)

*Koma ine ndatsimikizadi
kusonyeza mtima wosagawanika.*

2. Sindikhala ndi anthu oipa.
Ndimadana ndi onyoza choonadi.
Chonde musachotse moyo wanga
Ndi anthu oipa okonda ziphuphu.

(Kolasi)

3. Ndikonda kukhala m'nyumba yanu.
Ndimasangalala kukulambirani.
Ndidzayendadi kuguwa lanu,
Pokuyamikani mokweza kwambiri.

(Kolasi)

35 “Muzitsimikizira Kuti Zinthu Zofunika Kwambiri Ndi Ziti” (Afilipi 1:10)

1. Kuzindikira kudzatithandiza,
Kudziwa zoonu,
Kudziwa zomwe ndi zofunika,
Kuti tizizichita.

(KOLASI)

Uzidana ndi choipa.

Sangalatsa;

Mtima wa Mulungu,

Madalitso tidzapeza,

Tikamachita zofunika.

2. Palibe chofunika kuposa
Kulengeza uthenga,
Kufufuza a njala ya choonadi
N’kuwaphunzitsa.

(Kolasi)

3. Tikamachita zofunika,
Tidzakhala okhutira.
Mtendere wa Mulungu
Udzatetezatu maganizo.

(Kolasi)

36

Timateteza Mtima Wathu

(Miyambo 4:23)

1. Titeteze mtima wathu;
Tikhale ndi moyo.
M'lungu amadziwa bwino
Za mumtima mwathu.
Mtima ndi wonyenga,
Ungatisocheretsetu.
Choncho tiganize bwino
Timvere Yehova.
2. Timafunafuna M'lungu
Tikamapemphera.
Timathokozadi zonse,
Zomwe amachita.
Zimene amaphunzitsa
Timazitsatira.
Ndipo tikhulupirike
Timusangalatse.
3. Titeteze mtima wathu,
Tipewe zoipa.
Mawu a Yehova M'lungu,
Atitsogolere.
Anthu okhulupirika;
Amawakondadi.
Choncho timulambiretu
Monga bwenzi lathu.

*Kutumikira Yehova ndi
Moyo Wathu Wonse*
(Mateyu 22:37)

1. Yehova Wamphamvuyonse,
Inetu ndimakukondani.
Mtima wanga wonse umafuna;
Kukutumikirani.
Malamulo anu ndimvera,
Zofuna zanu ndichita.

(KOLASI)

*Inu Yehova ndinu woyenera
Kutumikiridwa.*

2. Atate zomwe munalenga
Zimakulemekezani.
Ndi mphamvu zangatu zonse,
Ndidzauza ena za inu.
Ndithandizenitu Yehova,
Kuti ndikhulupirike.

(Kolasi)

1. Panali chifukwa chimene Mulungu

Anakupatsira choonadi.

Anaona mtima wofuna kuchita

Zabwino zomusangalatsadi.

Unalonjeza kum'tumikira;

Ndipo iye anakuthandiza.

(KOLASI)

Ndi magazi a Yesu

Anakuwombola.

Ndiwe wa Mulungu,

adzakulimbitsa.

Adzakutsogolera

ndi mzimu woyera.

Adzakulimbitsa

adzakuteteza.

2. Mulungu anapereka Mwana wake;

Amafunatu zikuyendere.

Ngati Mwana wakeyo sanatimane

Kukulimbitsa sangalephere.

Chikondi chako sangaiwale;

Sangasiye ndithu anthu ake.

(Kolasi)

39 Tipange Dzina Labwino Ndi Mulungu

(Mlaliki 7:1)

1. Pamoyo wathu, Tsiku lililonse
Tipange dzina Labwino ndi M'lungu.
Tikachita zinthu Zabwino kwa M'lungu,
Tisangalatsa Mtima wake.
2. Kufunitsitsa Kutchuka m'dzikoli,
N'cholinga choti Anthu atikonde.
Kulibetu phindu Chifukwa Yehova,
Sangatikonde Tikatero.
3. Tifuna M'lungu Atilembe dzina
Kuti tikhale, Mu buku la moyo.
Choncho tikhaletu Ndi dzina labwino
Kwa M'lungu wathu, Nthawi zonse.

1. Iwe ndi wandani?

Umvera m'lungu uti?
 Amene umam'gwadirayo.
 Iye ndiye m'lungu wako.
 Milungu iwiri;
 Sungaitumikire.
 Sungalambire iwiri yonse,
 Sankhapo mmodzi yekha.

2. Iwe ndi wandani?

Umvera m'lungu uti?
 Zilitu ndi iwe kusankha,
 Woonu kaya wonama.
 Kodi Kaisara
 Udakamukondabe?
 Kapena udzamvera Yehova
 N'kugwira ntchito yake?

3. Ine ndi wandani?

Ndidzamvera Yehova.
 Atate wanga wakumwamba;
 Ine ndidzam'sangalatsa.
 Anandigulatu;
 Ndidzanutumikira.
 Ndizim'lambira, dzina lakenso
 Ndizililemekeza.

41 *Mulungu Imvani Pemphero Langa* (Salimo 54)

1. Atate mumve nyimbo yanga.
M'lungu wanga ine ndi wanu.
Dzina lanu ndi lalikulu.

(KOLASI)

Yehova mumve pempheroli.

2. Ndathokoza ndadzuka bwino,
Mwandipatsa mphatso ya moyo.
Mumandisangalatsa mtima.

(Kolasi)

3. Ndifuna kuchita zabwino.
Ndiyendetu m'kuwala kwanu.
Ndipirire mavuto onse.

(Kolasi)

42 Pemphero la Mtumiki wa Mulungu (Aefeso 6:18)

1. M'lungu, Atate, Wamphamvuyonse,
Dzina lanulo liyeretsedwetu.
Mumachita zomwe mwafuna,
Tikupempha Ufumu ubwere.
Pa nthawi yanu M'lungu,
Tidzadalitsidwetu.
2. Mumatichitiranso zabwino,
Mphatso zoti sitikanazipeza.
Ndinu Gwerodi la kuwala,
Mwatithandiza kupeza nzeru.
Tizikuthokozani,
Chifukwa cha chikondi.
3. Zotisautsa m'dziko n'zambiri
Tikupempha muzititonthozadi.
Nkhawa zathu tipatsa inu,
Muzitithandiza kupirira.
Malonjezo athunso,
Tiwakwanitse ndithu.

43 *Pemphero Loyamikira Mulungu* (Salimo 95:2)

1. Yehova tikukuyamikirani.
Kudzera mupemphero lathuli.
Mofunitsitsa tidzatumikira,
Timadziwa mumatithandiza.
Nthawi zina timakuchimwirani.
Tipempha mutikhululukire.
Tikuthokoza munatiwombola.
Mumadziwanso ndife ofo'ka.
2. Tikuyamika mumatikondatu.
Munatikokeranso kwa inu.
Mutidziwitse za inu Mulungu
Mutiphunzitse kukukondani.
Mzimu wanu umatithandizadi.
Timalankhula molimba mtima.
Titumikire modzichepetsadi;
Timakuthokozani Yehova.

44 *Pemphero la Munthu Wovutika* (Salimo 4:1)

1. Yehova ndipempha:

“Imvani pemphero langa.”

Zilonda zanga zakula;

sizipola msanga.

Kuvutika ndi maganizo

kwandifoola.

Ndichitireni chifundo M’lungu

wotonthoza.

(KOLASI)

Ndidzutseni; ndipirire.

Nkhawa zanga zichotseni.

Pamavuto n’thandizeni.

Yehova ndilimbitseni.

2. Ndikafo’ka Mawu anu

amanditonthoza,

Amafotokoza mfundo

zondigwira mtima.

Ndidziwe kuti chikondi chanu

n’chachikulu.

Ndikumbukire kuti

n’choposa mtima wanga.

(Kolasi)

45 *Kusinkhasinkha kwa Mtima Wanga* (Salimo 19:14)

1. Zomwe ndimasinkhasinkha,
Zimene ndimaganiza—
Zikusangalatseni Ya,
Kuti ndikhale wolimba.
Pamene ndili ndi nkhawa
N’kumalephera kugona,
Ndisinkhesinkhe za inu
Inde zinthu zoyenera.
2. Zilizonse zolungama,
Zofunika ndi zoonā,
Ndikamaziganizira—
Zindipezetse mtendere.
Nzeru zanu n’zofunika
Komanso ndi zochuluka.
Choncho ndizisinkhasinkha
Zonena zanu mwakhama.

46 *Timakuyamikirani Yehova* (1 Atesalonika 5:18)

1. Tikuyamikani Yehova M'lungu,
Mumatipatsa kuwala kwanu.
Tikuyamika mwayi wa pemphero,
Kuti tinene mavuto athu.
2. Tikuyamika potumiza Yesu,
Amene anagonjetsa dziko.
Tikuyamikani potithandiza
Kukwaniritsa lonjezo lathu.
3. Tikuyamika chifukwa cha mwayi
Wolalikira za dzina lanu.
Tiyamika mudzathetsa mavuto,
Madalitso anu sadzathadi.

47 *Muzipemphera kwa Yehova* *Tsiku Lililonse* (1 Atesalonika 5:17)

1. Pemphera kwa Yehova amamva.
Ndi mwayi umene watipatsa.
Umuuze zamumtima mwako,
Ndi wodalirika, bwenzi lako.
Pempherabe kwa M'lungu.
2. Pemphera kwa M'lungu uthokoze.
Tim'pemphe atikhululukire.
Timuuze zomwe talakwitsa,
Amadziwa zofooka zathu.
Pempherabe kwa M'lungu.
3. Pemphera kwa M'lungu zikavuta,
Ndi Tate wathu amathandiza.
Um'pemphe kuti akuteteze,
Um'khulupirire usaope.
Pempherabe kwa M'lungu.

48 *Tiziyenda ndi Yehova Tsiku Lililonse*

(Mika 6:8)

1. Timayenda ndi Atate,
Nthawi zonse modzichepetsa.
N'ngokoma mtima kwa anthu
Ochita zomusangalatsa.
Ndipo anakonza njira,
Kuti tiyende naye.
Choncho tidzipereketu,
Potumikira Yehova.
2. Mapeto ali pafupi,
Ndipo Satana ndi wokwiya.
Timatsutsidwa kwambiri,
Choncho tingamachite mantha.
Yehova atiteteza,
Tikamuyandikira.
Tim'tumikire kosatha,
Tim'konde ndi mtima wonse.
3. M'lungu akutithandiza,
Ndi mzimu ndi Mawu akenso.
Kudzera mu mpingo wake,
Amamvanso pemphero lathu.
Tikayenda ndi Yehova,
Tidzachita zabwino.
Choncho tikhulupirike,
N'kukhala odzichepetsa.

49 *Tizikondweretsa Mtima wa Yehova* (Miyambo 27:11)

1. M'lungu takulonjezani;
Kuchita zofuna zanu,
Tidzagwira ntchito yanu
Mtima wanu ukondwere.
2. Kapolo wanu padziko,
Amalengeza za inu
Amatipatsa chakudya,
Kuti tizikumverani.
3. Mutipatse mzimu wanu,
Kuti tikhulupirike
Ndipo tibale zipatso.
Tizikusangalatsani.

50

Pemphero Langa
Losonyeza Kudzipereka
(Mateyu 22:37)

1. Tengani mtima wanga
Cho'nadi uzikonda.
Tengani mawu anga
Ndikuimbirenitu.
2. Tengani mapaziwa;
Akutumikireni.
Chuma changa tengani.
Sindingakumaneni.
3. Tengani moyo wanga,
Chifuniro chanucho,
Ndizichichita ndithu
Ndikusangalatseni.

51 *Tadzipereka kwa Mulungu*

(Mateyu 16:24)

1. M'lungu wathu watikokera kwa Khristu
Kuti azititsogolera.
Cho'nadi tachidziwa,
M'lungu watiphunzitsa.
Ndipotu tadzikana,
Tipita patsogolo.

(KOLASI)

*Ifetu tadzipereka kwa Mulungu.
Ndipo tikusangalala zedi.*

2. Tamulonjezatu Yehova m'pemphero
Kuti tidzamutumikira.
Tilidi ndi chimwemwe,
Timauzanso ena,
Za dzina la Yehova,
Ndi Ufumu wakenso.

(Kolasi)

52 *Kudzipereka Monga Mkhristu* (Aheberi 10:7, 9)

1. Yehova analengatu
Chilengedwe chonse,
Dzikoli ndi mlengalenga,
Zonsezi ndi zake.
M'lungu watipatsa moyo
Wasonyeza kuti
Ndi woyenera kum'tamanda,
Ndiponso kum'lambira.
2. Yesu anabatizidwa
N'kunena m'pemphero:
'Ndabwera kuti ndichite
Chifuniro chanu.'
Anatuluka m'Yo'dano
Monga wodzozedwa,
Kuti atumikire M'lungu
Monga wodzipereka.
3. Yehova, ife tabwera
Kukutamandani.
Tadzipereka kwa inu
Ndipo tadzikana.
Yesu munamupereka,
Monga dipo lathu.
Tasiyatu zofuna zathu,
Tizichita za inu.

53 *Kukonzekera Kupita Kolalikira* (Yeremiya 1:17)

1. Tsopano
Kunja kwacha,
Tikalalikiretu.
Komano mvula,
Yayambanso kugwa.
N'zosavuta kupitiriza
Kugona.

(KOLASI)

*Tisafo'ke tikonzekere,
Tipemphe Yehova,
Iye angatilibikitse
N'zofunika.
Tipezenso woyenda naye
Wotilibikitsa.
Angelo amatithandiza
Osafo'ka.*

2. Chimwemwe

Tidzapeza,

Ngati sitingafo'ke.

Ndipo Yehova

Amaona zonse

Sangaiwalenso chikondi

chathuchi.

(Kolasi)

“Njira Ndi Iyi”
(Yesaya 30:20, 21)

1. Pali njira imene,
Munaidziwa,
Njira yamtendere
Munaiphunzira
Pamene munamvera
Mawu a Yesu,
Ndi njira yopezeka
M’Mawu a M’lungu.

(KOLASI)

*Njira yakumoyo ndi yomweyi.
M’sacheuke m’sapite kumbali!
Mawu a Mulungu akuti:
‘M’sapatuke njira ndi yomweyi.’*

2. Pali njira imene
Ndi yachikondi,
Tikaitsatira
Timaona kuti
Chikondi cha Mulungu
ndi chochuluka.
Njirayi yachikondi;
Imatikhudza.

(Kolasi)

3. Pali njira ya moyo
Imodzi yokha.
Palibe inanso
M'lungu walonjeza:
Ndi yokhayi
Tingapezemo chikondi.
Njira yakumoyotu
Ndi imeneyi.

(Kolasi)

Musawaope! (Mateyu 10:28)

1. Pitanibe anthu anga,
Lengezani Ufumu.
Musaope mdaniyo.
Dziwitsani achidwi
Kuti Mwana wanga Yesu,
Wagwetsadi mdaniyo,
Posachedwa adzam'manga,
Sadzazunzanso anthu.

(KOLASI)

*Musaope anthu anga,
Kaya akuopseni.
Ndidzakutetezerani
Monga mwana wa diso.*

2. Adani angachuluke,
Ndi kukuopsezani,
N'kukunyengererani,
Kuti mupusitsidwe.
Musaope anthu anga,
Kaya akuzunzeni,
Ndidzakutetezerani
Mpaka onse atatha.

(Kolasi)

3. Sindingakuiwaleni,
 Ndidzakutetezani.
Ngakhale akupheni,
 Ndidzagonjetsa imfa.
Musaope opha thupi
 Sangawononge moyo.
Choncho khulupirikani;
 Mudzalandira moyo.

(Kolasi)

56

Inuyo Panokha Muzikonda Kwambiri Choonadi

(Miyambo 3:1, 2)

1. Njira yabwino ndiyo ya choonadi
Wina sangakusankhireni.
Choncho malangizo a M'lungu mverani,
Ndipo m'khulupilireni.

(KOLASI)

*M'konde cho'nadi,
Chikhale chanuchanu.
Ndipo mudzakhala
Achimwemwe
M'kamakonda cho'nadi.*

2. Mukatumikira Mulungu mwakhama
Mudzalandira madalitso,
Komanso mudzapeza moyo wosatha,
Wamtendere ndi wabwino.

(Kolasi)

3. M'maso mwa M'lungu tilitu ngati ana
Ofunika kulangizidwa.
Tiyende naye Atate wakumwamba,
Choncho tidzadalitsidwa.

(Kolasi)

Tizilalikira kwa Anthu a Mitundu Yonse

(1 Timoteyo 2:4)

1. Timutsanzire Mulungu wathu
Pokhala anthu opanda tsankho.
Akufuna kuti anthu onse,
Amve uthenga, apulumuke.

(KOLASI)

*Wofunika ndi munthu,
Osati mtundu wake.
Tiphunzitse onse mosasankha
Timakondatu anthu,
Tiwauze uthenga
'Akhale mabwenzi a Yehova.'*

2. Kulikonse angapezekeko,
Kaya akuoneka motani,
Mtima wawo ndiwo wofunika.
Yehova amaona mtimawo.

(Kolasi)

3. Yehova amalandira anthu
Omwe asankha kum'tumikira.
Choncho anthu a mitundu yonse,
Tiwauze uthenga wabwino.

(Kolasi)

58 *Kufufuza Anthu Okonda Mtendere*

(Luka 10:6)

1. Yesu anatilamula kuti

tiuze anthu uthenga.

Amve mawu a Yehova.

Ankakonda nkhosa za Mulungu.

Ankazifufuza

mwakhama tsiku lonse.

Nyumba ndi nyumba, mumsewu

Timauza aliyense,

Kuti posachedwa mavuto atha.

(KOLASI)

Tifufuze

okonda mtendere m'dzikoli.

Tiwapeze

Ofuna kupulumutsidwa.

Tifufuze

Paliponse.

2. Tifufuzabe anthu mwa khama.

Alipo ambiri

omwe tingathe kuwathandiza.

Poti timawakonda kwambiri,

Tibwererekonso

Tikawalimbikitse.

M'matauni, ndi m'midzinso,

Tikapeza omvetsera,

Timasangalala powaphunzitsa.

(Kolasi)

59 *Tamandani Ya Limodzi ndi Ine* (Salimo 146:2)

1. Titamande;

Ya mokweza!

Amatipatsa zonse zabwino.

Tsiku lonse,

Tim'tamande,

Ndi wachikondi, n'ngwamphamvu zonse.

Ndipo dzina lake tilengeze.

2. Titamande;

Ya chifukwa.

Amatimva tikamapemphera.

Dzanja lake

Ndi lamphamvu;

Amalimbikitsa ofooka.

Za mphamvu zake timalengeza.

3. Titamande;

Ya mokondwa.

N'ngolungama ndi wodalirika.

Adzakonza

Zolakwika.

Ndipo anthu adzadalitsidwa.

Timutamande mosangalala!

1. Mulungu akufuna
tichenjeze anthu
Kuti tsiku la mkwiyo
wake likubwera.

(KOLASI)

*Akamvera adzapeza,
Inde moyo wosatha.
Nafe tidzapulumuka,
Tikafalitsa uthenga,
Uthenga.*

2. Tili ndi uthenga
woti tiuze anthu.
Tiitane anthu abwere
kwa Mulungu.

(Kolasi)

(VESI LOKOMETSER)

*Mwamsanga tilengeze,
Anthu amve, aphunzire.
Cho'nadi tiphunzitse,
Kuti moyo adzapeze.*

(Kolasi)

61 *Pitani Patsogolo Mboninu*

(Luka 16:16)

1. Olimba m'nthawi yamapeto ino,
Ndi atumiki oteteza uthenga.
Mdyerekezi amawatsutsa.
Mumphamvu ya Yehova samagonja.

(KOLASI)

*Ndiye pitani patsogolo Mboninu!
Kondwerani pogwira ntchito ya M'lungu!
Uzani onse zadziko latsopano
Mmene mudzakhala madalitso.*

2. Tisatengeke ndi moyo wofewa,
Kusangalatsa dzikoli tizipewa.
Mawanga a dziko tikane
Ndi kukhala okhulupirikabe.

(Kolasi)

3. Ufumu wa M'lungu ukunyozedwa,
Dzina lake loyera likudetsedwa.
Tiyenitu tiliyeretse,
Kumitundu yonse tililengeze.

(Kolasi)

Nyimbo Yatsopano (Salimo 98)

1. Imbira M'lungu, Imba nyimbo yatsopano.
Unene kwa onse Ntchito zake zonse.
Umutamande, Mulungu ndi wopambana.
Poweruza anthu
Ndi wachilungamo.

(KOLASI)

Imbani!

Nyimbo yatsopano.

Imbani!

Yehova ndi Mfumu.

2. Fu'la mokondwa, Fuula kwa Mfumu yathu!
Mutamandenitu, Ndi nyimbo mokondwa.
Tiyeni tonse Timuimbire mokweza.
Zeze ndi lipenga
Ziimbe pamodzi.

(Kolasi)

3. Nyanja ndi zinthu Za mmenemo zim'tamande.
Inde zolengedwa, Zonse zim'tamande.
Mtunda ukondwe, Mitsinjenso ikondwere.
Mapiri ndi zigwa,
Nazo zim'tamande.

(Kolasi)

1. Apanga timilungu,
M'lungu wo'na sam'dziwa.
Ndi Wamphamvuyonse,
Monga tidziwa.
Milunguyo sidziwa,
Zomwe zili m'tsogolo.
Milunguyo ilibe mboni,
Chifukwatu ndi yabodza.

(KOLASI)

*Mboni za Yehovafe.
Tina mosaopa.
M'lungu wathu akalosera;
Ndithu zimachitika.*

2. Timalengeza dzina
La Yehova Mulungu.
Ndi Ufumu wake,
Molimba mtima.
Timathandiza ena,
Kudziwa choonadi.
Akamalimba adzaimba,
Nyimbo yotamanda M'lungu.

(Kolasi)

3. Ntchito yolalikira,
Za dzina la Yehova.
Imachenjezadi,
Olidetsawo.
Imathandiza anthu,
Kukhululukidwadi.
Imabweretsanso chimwemwe,
Komanso chiyembekezo.

(Kolasi)

64 *Tizigwira Ntchito Yokolola* *Mosangalala* (Mateyu 13:1-23)

1. Tili munthawi yokolola,
Ndi mwayidi waukulu.
M'mindamo tirigu wachanso,
Tiyenitu ticolole.
Yesu akutitsogolera,
Ndi chitsanzo chabwinotu.
Timakhala osangalaladi.
Kugwira nawo ntchitoyi.
2. Timakonda M'lungu ndi anthu,
Choncho timachita khama.
Tiphunzitse anthu mwachangu,
Mapeto ayandikira.
Yehova amatidalitsa,
Timakhala achimwemwe.
Tipirire pogwira ntchitoyi,
M'lungu adzatithandiza.

1. Pita patsogolo khala wolimba!
Onetsa kuwala anthu onse aone.
Sonyezatu luso muutumiki;
M'lungu adzathandiza.
Utumikiwu ndi wa onse.
Yesu naye anauchita.
Dalira Mulungu kuti usagwe,
Gwiritsa chilungamo.

2. Pita patsogolo molimba mtima!
Uzilalikira ku mtundu uliwonse.
Tamanda Yehova Mfumu yathuyo,
Polalikira nawo.
Adani angatiopseze,
Tisaleke, onse amvetu.
Kuti Ufumu wa M'lungu wayamba.
Phunzitsa choonadi.

3. Pita patsogolo usabwerere,
Wonjezera luso
ntchito ndi yaikulu.
Mzimu wa Mulungu ukuthandize,
Udzapeza chimwemwe.
Konda anthu omwe wapeza.
Bwerera, uwafike m'mtima.
Athandize apite patsogolo,
Cho'nadi chiziwala.

66 *Lengezani Uthenga Wabwino*

(Chivumbulutso 14:6, 7)

1. Poyamba sitinkadziwa za Ufumu.

Pano tikudziwa Mfumu yalonjezo.

Mwa chifundo ndi chikondi cha Yehova,

Anaganizira anthu ochimwafe.

Anakonza zoti Yesu alamule;

Ufumuwo unali

woti udzabadwe.

Komanso kusankha kagulu ka nkhosa,

Kadzakhale mkwatibwi wa Mwana wake.

2. Mulungu ankadziwa za uthengawu.

Pano akufuna anthu audziwe.

Angelo amakondwa potithandiza

Kugwira ntchito yolengeza Ufumu.

Tilitu ndi udindo ndiponso mwayi

Wom'tamanda ndi kuyeretsa

dzina lake.

Tili ndi mwayi wolengeza dzinalo

Mwa kulalikira uthenga wabwino.

1. Mulungu watilamula;
Ndipo tikufunika kumvera.
Tifotokozeretu anthu
Adziwe chiyembekezo chathu.

(KOLASI)

Lalikira

Indetu onse amve!

Lalika,

Dzikoli lisanathe.

Lalika,

Ofatsa amvetsetse.

Lalika

M'dziko lonse!

2. Mavuto adzatiyesa;
Tingapezeke tikunyozedwa.
Kulalikira kungavute,
Tidzakhulupirirabe M'lungu.

(Kolasi)

3. Nthawi zina tidzapeza,
Anthu ofunadi kumvetsera.
Tiwaphunzitsa 'pulumuke
Dzina la Yehova tiyeretse.

(Kolasi)

1. Bwerani mudzagwire ntchito;
Yotumikira Ambuye.
Iye adzakuthandizani;
Mukamvera malangizo.
Mbewu za cho'nadi zidzakula
M'mitima ya omvetsera.
Choncho tumikirani mwakhama
Pa ntchito imene mwapatsidwa.

2. Kuti ntchito iyende bwino
Zingadalire inuyo.
Mukaphunzitsa bwino anthu
Adzakondatu cho'nadi.
Muwathandizetu kupirira
Mavuto apadzikoli.
Mudzasangalalatu kuona
Akukonda cho'nadi kwambiri.

69 *Pitirizani Kulalikira za Ufumu* (2 Timoteyo 4:5)

1. Pitani patsogolo ndithu
Polalikira konse.
Muthandize anthu ofatsa,
Akonde choonadi.
Ndi mwayidi kutumikira;
Tikonde kulalikira.
Chitirani umboni M'lungu;
Ndi dzina lake loyera.

(KOLASI)

*Pitirizani kulalikira
padziko lonse.
Pitirizani kukhala
okhulupirikabe.*

2. Tipite patsogolo tonse,
Amuna ndi akazi.
Odzozedwa ndi nkhosa zina
Tisasiye cho'nadi.
Ndi kofunika kuti anthu
Amve uthenga wabwino.
Yehova atipatsa mphamvu;
Ndipo sitiopa kanthu!

(Kolasi)

1. Ambuye wathu anatisonyeza,
Njira yolalikirira:
'Fufuzani anthu oyenerera,
Ofuna kumva choonadi.
Muziwapatsa moni eni nyumba,
Ndi kuwafunira mtendere.
Ngati sanakulandireni,
Sasani fumbi m'mapazi muchoke.'
2. Onse amene akulandirani,
Alandiranso Ambuye.
Ahandizeni kusonyeza mtima
Wofuna kudziwa cho'nadi.
Musadere nkhwawa zoti munene,
Yehova akuthandizani.
Mawu anu akakhala okoma
Ofatsa adzasangalala.

71 *Ndife Gulu Lankhondo la Yehova* (Aefeso 6:11-14)

1. Ndife gulu lankhondo,
La M'lungu wathu.
Lotsogoleredwa ndi
Mwana wake Yesu.
Satana angatsutse,
Tilalikabe.
Ndife osaopa
Olimba mtima.

(KOLASI)

Ndife gulu lankhondo.

Tikulengeza:

“Ufumu wayamba

Kulamulira.”

2. Ndife anthu a M'lungu,
Ofunafuna,
Anthu omwe ndi nkhosa,
Zosowa za M'lungu.
Tifuna kuwapeza,
N'kuwaphunzitsa,
N'kuwalimbikitsa:
“Tizisonkhana.”

(Kolasi)

3. Ndife gulu lankhondo,
Lomvera Yesu,
Lokonzekera nkhondo,
Lolimbatu mtima.
Koma tikhale tcheru,
Kuti tisagwe.
Zinthu zikavuta,
Tisafooke.

(Kolasi)

*Tikulalikira Choonadi
Chonena za Ufumu*
(Machitidwe 20:20, 21)

1. Poyamba sitinkadziwa
Zinthu zoti tizichita.
Yehova 'natumiza
Choonadi ndi kuwala.
Ndipo tinazindikira
Chifuniro cha Yehova,
Kuti tim'tumikire
Ndi kumalengeza dzina lake.
Timalalikira ndithu
Pamakomo ndi mumsewu.
Timathandiza anzathu
Choonadi achidziwe.
Tiyeni tiziyesetsa
Kutumikira Mulungu,
Kufikira Yehova
Atanena kuti tamaliza.

73 *Tithandizeni Kukhala Olimba Mtima*

(Machitidwe 4:29)

1. Polalikira Ufumu,
Kukweza dzina lanu,
Anthu ena amatsutsa,
Ndiponso kutinyoza.
Koma sitiwaopa,
Timamvera inu nokha.
Choncho Yehova, tikupempha;
Mutipatse mzimu wanu.

(KOLASI)

*Polalikira uthenga,
Mutichotsere mantha.
Tikhale olimba mtima
Anthu amve uthenga.
Amagedo ikufika,
Tikhale olimba mtima,
Tithandizeni Yehova.
Tikupempha.*

2. Pamene tichita mantha,
Mudziwa ndife fumbi.
Mudzatithandiza ndithu
Paja munalonjeza.
Imvani kuopseza,
Kwa anthu odana nafe.
Tithandizeni, tisaope
Tikhale olimba mtima.

(Kolasi)

Tiyeni Tiimbire Limodzi
Nyimbo ya Ufumu
 (Salimo 98:1)

1. Iyi ndi nyimbo yachisangalalo;
 Yolemekeza M'lungu wamkulu.
 Imatipatsadi chiyembekezo.
 Imbani nafe nyimbo yathuyi:

(KOLASI)

*'Lambirani M'lungu wathu,
 Mwana waketu ndi Mfumu!
 Dzaphunzireni nyimbo ya Ufumu
 Tamandani dzina la Mulungu.'*

2. Ndi nyimboyi tilengeza Ufumu.
 Khristu Yesu ndi wolamulira.
 Ndipo mtundu watsopano wabadwa
 Nawo ukumusangalalira.

(Kolasi)

3. Nyimboyi omwe angaiphunzire,
 Ndi amene amadzichepetsa.
 M'dziko lonse ambiri aphunzira.
 Akuitananso anthu ena.

(Kolasi)

75 “Ine Ndilipo! Nditumizeni!”

(Yesaya 6:8)

1. Lero anthu akunyoza
Dzina loyera la M’lungu.
Ena amati n’ngwankhanza.
Enanso: “Kulibe M’lungu.”
Ndani adzaliyeretsa,
Dzina la Yehova M’lungu?

(KOLASI 1)

*‘Ndilipo! Nditumizeni!
Ndidzaimbira inuyo.
Ndi mwayi waukulu, Mbuye.
Ine! Nditumizeni!’*

2. Anthu osaopa M’lungu;
Akumati akuchedwa.
Amalambira mafano,
Ena eti Kaisara.
Ndani adzawachenjeza
Za nkondo ya M’lungu wathu?

(KOLASI 2)

*'Ndilipo! Nditumizeni!
N'dzachenjeza mosaopa.
Ndi mwayi waukulu, Mbuye.
Ine! Nditumizeni!'*

3. Anthu ofatsa 'kulira
Zoipa zikuchuluka.
Iwo amafunitsitsa
Choonadi chomasula.
Ndani adzawatonthoza?
Ndani adzawathandiza?

(KOLASI 3)

*'Ndilipo! Nditumizeni!
Ndidzaphunzitsa ofatsa.
Ndi mwayi waukulu, Mbuye.
Ine! Nditumizeni!'*

1. Kodi m'mamva bwanji
 m'kazindikira kuti,
 mwasonyezadi khama
 pophunzitsa ena?
 Inde m'kayesetsa,
 M'lungu adzadalitsa.
 Mudzathandiza anthu
 kudziwa Mulungu.

(KOLASI)

*Timasangalala ndithu
 kupereka mtima wathu.
 Choncho tim'tumikirebe
 tsiku lililonse.*

2. Kodi m'mamva bwanji
 m'kazindikira kuti,
 mwawafika pamtima
 akamva uthenga?
 Ena amakana,
 ena kunamizidwa.
 Koma timanyadira
 tikalalikira.

(Kolasi)

3. Kodi m'mamva bwanji
m'kakumbukira kuti,
mwa chikondi Yehova
amatsogolera?

Timalalikira,
anthu timaphunzitsa,
akhale ndi tsogolo
adzapeze moyo.

(Kolasi)

1. M'dzikoli mulitu mdima,
Anthu sakumvera.
Koma taona kuwala,
Ngati m'bandakucha.

(KOLASI)

*Uthenga wa M'lungu,
Wawala ngati dzuwa
M'dziko lamdimali.
Ukupatsa anthu
Onse chiyembekezo
Mdimu watha.*

2. Tidzutse omwe agona,
Poti nthawi yatha.
Ndipo tiwalimbikitse,
Tiwapempherere.

(Kolasi)

78 “Kuphunzitsa Mawu a Mulungu” (Machitidwe 18:11)

1. Ophunzitsa choonadi,
Amasangalala.
Timapeza madalitso
Ochuluka ndithu.
Timatsanziratu Yesu
Pophunzitsa ena.
Ndipo timawathandizatu
Kukonda Mulungu.
2. Pamene tikuphunzitsa,
Tichite zabwino,
Anthu onse aonetu
Kuwala kwa M’lungu.
Timafufuza mwakhama,
Mawu a Mulungu.
Pouza ena uthengawu
Timaphunziranso.
3. Zofunika pophunzitsa
M’lungu watipatsa.
Ndipo tikamamupempha,
Adzatithandiza.
Timakonda Mawu ake;
Omwe ndi oona.
Tikakonda ophunzira,
Adzatumikiranso.

79 *Athandizeni Kukhala Olimba*

(Mateyu 28:19, 20)

1. Kuphunzitsa nkhosa za M'lungu

Ndi mwayi wapadera.

Yehova wawatsogolera

Amakonda cho'nadi.

(KOLASI)

Yehova tikupemphatu

Kuti muziwateteza.

Mwa Yesu tikupemphani: Athandizenibe

Akhale olimba.

2. Mayesero akawagwera,

Tinkawapempherera.

Tinawaphunzitsa mwakhama;

Pano adalitsidwa.

(Kolasi)

3. Akhale okudalirani,

Inu M'lungu ndi Yesu.

Apirire pamayesero,

Akalandire moyo.

(Kolasi)

80 “*Talawani Ndipo Muona Kuti Yehova Ndi Wabwino*” (Salimo 34:8)

1. Kutumikira Mulungu;
Kumatisangalatsadi.
Ntchito n’njambiri yolalikira,
Timaipezera nthawi.

(KOLASI)

*M’lungu akuti: ‘Talawani—
Inetu ndi wabwino.’
Timapindula tikachita,
Zonse zomwe tingathe.*

2. Mtumiki wanthawi zonse,
M’lungu amamudalitsa.
Amamupatsa zofunikira,
Amakhala wokhutira.

(Kolasi)

1. M'mawa uliwonse, tulo tisanathe,
Timadzuka n'kupita
kolalikira uthenga.

Ndipo Mulungu amatitsogolera
Timakondwa anthu
akamamvetsera uthenga.

(KOLASI)

*Tinasankha,
kutumikira Yehova.
Timachita zofuna zake.
Tipitirizabe kulalikiraku,
Tikatero timasonyeza
Chikondi.*

2. Pofika madzulo, timatopa ndithu,
Komabe timapeza
chimwemwe potumikira.

Madalitso Yehova amatipatsa
Nthawi zonse
timamuthokoza potithandiza.

(Kolasi)

1. Yesu walamula
Kuti tiwale,
Monga dzuwa
limawalira onse.
Mawu a mtendere,
Ali m’Malemba.
Choncho tizisonyeza
Kuwala kwa Ya.
2. Uthenga wa M’lungu
Onse amvetu,
Uzitiwalira
Polalikira.
Mfundo za cho’nadi
Zitsogolere.
Anthu asankhe okha,
Kumva uthenga.
3. Tikamasonyeza
Kukoma mtima,
Timawalitsadi
Dziko la mdima.
Choncho tisonyeze
Kuwala kwathu,
Tikatero Mulungu
Asangalala.

1. Kunyumba ndi nyumba
Ife timalalikira.
Kulikonse nkhusa za M’lungu,
Zikudyetsedwa.
Zoti Ufumu wa M’lungu
Ukulamulira,
Akhristu, tikulengeza
Akulu ndi ana.
2. Khomo ndi khomo,
Tinene za chipulumutso.
Dzina la M’lungu aitane
Apulumuke.
Adzaitana bwanji
Dzina lomwe sadziwa?
Choncho kumakomo awo
Tidzalilengeza.
3. Khomo ndi khomo
Tiyeni tifalitse mawu.
Asankhe okha kumvera,
Kapena kukana.
Koma dzina la Yehova
Tidzallengezabe.
Ndipo potero,
Tidzapezadi nkhusa zake.

1. Yehovatu watipatsa
zomwe timafunikira.
Kuti tizisangalala
pomwe tikum'tumikira.

(KOLASI)

*Timadzipereka,
pom'tumikira.
Ndipo kulikonse tipita,
mofunitsitsa.*

2. Padzikoli pali ntchito.
Kosowa tidzapitako.
Tikatero tisonyeza.
kuti ena timakonda.

(Kolasi)

3. Komwe tili kuli ntchito,
inde, zofunika luso.
Zinenero taphunzira.
Ena tikulalikira.

(Kolasi)

1. Takulandirani inu nonse
Mwasonkhana kuti m'phunzire.
Cho'nadi M'lungu amatipatsa;
Timavomera akamatiitana.
2. Tikuyamikira abalewa
Chifukwa amatilandira.
Ndi amenewa tizikondana,
Tilandirensa ena odzasonkhana.
3. Aliyense akuitanidwa,
Ndi M'lungu kudzaphunzitsidwa.
M'lungu watikokera kwa lye.
Choncho landiranani ndi mtima wonse.

86 *Tikhale Anthu Ophunzitsidwa*

(Yesaya 50:4; 54:13)

1. Bwerani mosangalala muphunzire.
“Bwerani m’dzamwe madzi a moyo.”
Dzadyeni inu nonse anjala.
Mudzalandiretu malangizo.
2. Tisaleketu kusunkhana pamodzi,
Tiziphunzitsidwa ndi Mulungu.
Kuno n’kumene kuli abale,
Kuno kulitu mzimu wa M’lungu.
3. Lilime lophunzitsidwa choonadi.
N’losangalatsa kulimvetsera,
Tipezeke ndi anthu a M’lungu,
Tizipezeka pamisonkhano.

1. Tikukhala m'dziko lomwe n'loipa;
Anthu sakudziwa M'lungu.
Choncho tifunikatu malangizo,
Oti atitsogolere.

Misonkhano yathu imathandiza;
Kukhala osangalala.
Timamvako mawu olimbikitsa
Cholinga tisafooke.

Sitidzasiya kugwiritsa ntchito;
Malamulo a Yehova.
Pamisonkhano timalangizidwa;
Kukondatu choonadi.
2. Yehova amadziwa bwino zinthu;
Zomwe tikufunikira.
Tikamasonkhana timasonyeza
Kuti timamudalira.

Malangizo ochoka kwa akulu,
Amatithandiza zedi.
Timadziwa kuti sitili tokha,
Iwo adzatithandiza.

Choncho poyembekezera m'tsogolo,
Tisasiye kusionkhana.
Tiziphunzira kugwiritsa ntchito
Nzeru yochoka kumwamba.

1. Yehova tasonkhanatu pamodzi,
Pomvera kuitana kwanu.
Mawu anu ndi nyale m'njira yathu,
Amatiphunzitsa za inu.

(KOLASI)

*Ndiphunzitseni njira zanuzo;
Ndikhale womvera malamulo.
Ndiyendetseni m'njira yoona,
Malamulo anu ndizikonda.*

2. Nzeru zanu Yehova ndi zakuya,
Mfundo zanu n'zolimbikitsa.
Mawu anu adzakhala kosatha,
Timapezamo zodabwitsa.

(Kolasi)

*Khalani Omvera
Kuti Mulandire Madalitso
(Luka 11:28)*

1. Kodi timamveradi Yesu Khristu
Pa zonse zimene ananena?
Zomwe anaphunzitsa ndi zabwino.
Tidalitsidwa tikazimvera.

(KOLASI)

*Mvera udalitsidwe
Kuti usangalale.
Zomwe Mulungu angakuuze,
Mvera udalitsidwe.*

2. Monga nyumba yomangidwa pathanthwe
Osati yomangidwa pamchenga.
Zochita zathu zingatiteteze,
Kokha ngati Yesu timumvera.

(Kolasi)

3. Monga mtengo wamumbali mwa madzi
Umabereka nthawi 'kafika,
Tikamvera tidzadalitsidwadi,
Moyo wosatha tidzalandira.

(Kolasi)

1. Pomwe tikulimbikitsana
Kutumikira Yehova,
Chikondi chathu chimakula;
Ndipo timagwirizana.
Chikondi cha anthu a M'lungu
N'chothandiza kupirira.
Timatetezedwa kwambiri,
Tikamakhala mumpingo.
2. Mawu a pa nthawi yabwino
Amalimbikitsa ndithu.
Mawu awa olimbikitsa
Amachoka kwa abale.
Kugwirira ntchito limodzi
Kumatisangalatsadi.
Tikhaletu olimbikitsa
Ndiponso othandizana.
3. Pamene tsiku la Yehova
Layandikira kwambiri,
Tifunika tizisonkhana
Kuti tiyende ndi M'lungu.
Tigwirizane ndi abale
Titumikire limodzi.
Choncho timalimbikitsana
Kuti tikhulupirike.

Ntchito Yomwe Tagwira Chifukwa cha Chikondi

(Salimo 127:1)

1. Yehova tikufuna;
Kupemphera mokhudzidwa.
Chifukwa mwatikonda,
Ndipo tasangalala.
Taona mwadalitsa,
Ntchito imene tagwira.
Ndipo tamangadi nyumbayi,
Mwatithandiza.

(KOLASI)

Kukumangirani nyumbayi

Yehova unali mwayi.

Nthawi zonse tilemekeze dzina lanu

Ndi kukutumikirani.

2. Mabwenzi achimwemwe,
Taonani tawapeza.
Sitidzaiwala mpakana
M'moyo wosatha.
Taona mzimu wanu,
Mukugwirizana kwathu.
Mwayi taupeza wokwezadi;
Dzina lanu.

(Kolasi)

92 *Malo Odziwika ndi Dzina Lanu*

(1 Mbiri 29:16)

1. Yehova ndi mwayi wathudi,
Kukumangirani nyumba.
Tikukupatsani tsopano
Idziwike m'dzina lanu.
Zonse zomwe timapereka
Zinalitu kale zanu.
Luso, mphamvu ndi chuma chatu,
Timapereka mokondwa.

(KOLASI)

*Tikupereka malowa,
Kuti mudziwikedi.
Tikupereka malowa;
Chonde alandireni.*

2. Tikulemekeza inuyo,
Pokutamandani pano.
Landirani ulemerero
Tikamachuluka muno.
Malowa tikukupatsani,
Tidzawasamalirabe.
Ndipo apereke umboni,
Inde mpaka kalekale.

(Kolasi)

93 *Mudalitse Msonkhano Wathu* (Aheberi 10:24, 25)

1. Pamsonkhanowu Yehova,
Tipempha m'tidalitse.
Ndifetu oyamikira;
Mzimu ukhale nafe.
2. M'tithandize kumvetsetsa;
Mfundo za choonadi.
M'tiphunzitse kulalika;
Tikhale achikondi.
3. Mudalitse misonkhano;
Mutipatse mtendere.
Mawu ndi zochita zathu
Zikulemekezeni.

*Timayamikira Mulungu
Potipatsa Mawu Ake*
(Afilipi 2:16)

1. Yehova Atate, tikuthokoza
Chifukwa Mawu anu mwatipatsa.
Munawauziradi;
Anatimasula.
Kuwala kwake kwatipatsa nzeru.
2. Mawu anu ndi amphamvu kwambiri.
Maganizo n'zolinga 'lekanitsa.
Ndiponso malamulo,
Anu n'ngolungama.
Mfundo zanu zimatitsogolera.
3. Mawu anu M'lungu, amatikhudza.
Aneneri anu anali anthu,
Chonde tithandizeni
Tikhulupirire.
Mwatipatsa Mawu, tathokoza Ya.

95 *Kuwala Kukuwonjezerekabe* (Miyambo 4:18)

1. Aneneri akale ankafuna,
Kudziwa za Yesu Mesiya.
Mzimu wa M'lungu unaneneratu,
Kuti adzatipulumutsa.

Nthawi yakwana, akulamulira,
Umboni wake ulipo.
Kudziwa zimenezi ndi mwayi
Waukulu womwe tili nawo.

(KOLASI)

*Kuwala kwa panjira yathu;
Kukuwonjezerekadi.
Zomwe M'lungu akuulula;
Zimatitsogoleradi.*

2. Ambuye wathu wasankha kapolo,
Ndi mmene amatidyetsera.
Ndipo kuwala kwa cho'nadi pano
Kukungowonjezerekabe.

Pano tikuyenda molimba mtima,
Mowala ngati masana.
Tikuthokoza Yehova chifukwa,
Cho'nadi chake watipatsa.

(Kolasi)

1. Pali buku limene mawu ake,
Amatibweretsera chimwemwe.
Mfundo zake zodabwitsa n'zamphamvu;
Zimathandiza 'khungu kuona.
Bukuli ndi Baibulo loyera.
Olilemba anauziridwa,
Ankakonda Yehova M'lungu wawo,
Mzimu wake unawathandiza.
2. Analemba zokhudza chilengedwe,
Mmene M'lungu anachilengera.
Analembanso za Paradaiso
Ndiponsotu mmene anathera.
Analemba za mngelo winawake
Amene ananyoza Yehova.
Zinabweretsa chisoni pa anthu,
Koma Yehova adzapambana.

3. Masiku ano tikusangalala

Ufumu wa Mulungu wayamba.
Yehova 'kupatsa chipulumutso
Kwa onse omwe amamukonda.
M' buku lake muli zosangalatsa;
Chakudya chamwanaalirenji.
Limatipatsa mtendere wambiri;
N'lofunika kuliwerengadi.

97 *Mawu a Mulungu Amatithandiza Kukhala ndi Moyo* (Mateyu 4:4)

1. M'moyo wathu timafuna,
Mawu a Mulungu.
Azititsogoleratu;
M'zonse timachita.
Ndipo tidzasangalala,
Ndi kudalitsidwa.

(KOLASI)

*Chakudya chofunikadi;
Ndi Mawu a M'lungu.
Moyo wathu ufunika;
Mawu a Mulungu.*

2. M'mawuwo timawerenga
Za anthu akale.
Omwe anatumikira—
Mokhulupirika.
Tikawerenga nkhanizi
Zimalimbikitsa.

(Kolasi)

3. Tikamawawerengatu,
Tsiku lililonse.
Tidzathadi kupirira,
Mayesero onse.
Ndiye tizikumbukira
Zomwe tawerenga

(Kolasi)

98 Malemba Anauziridwa ndi Mulungu

(2 Timoteyo 3:16, 17)

1. M'dzikoli, Mawu a M'lungu,
Amatiunikira.
Tikawagwiritsa ntchito,
Tidzakhala omasuka.
2. Mawu ndi ouziridwa,
Amatiphunzitsadi.
Amawongoladi zinthu,
Ndiponso kutilangiza.
3. Mawu a Mulungu wathu,
Amatiphunzitsatu.
Ngati timawawerenga
Azititsogoleradi.

Khamu la Abale
(Chivumbulutso 7:9, 10)

1. Abale ambirimбири,
 Inde ochuluka,
 Aliyense ndi mboni,
 Yokhulupirika.
Tilipodi ambiri,
 Tikuchulukabe,
 Tachokeratu ku mafuko,
 Ndi mitundu yonse.
2. Abale ambirimбири,
 Timalalikira
 Uthenga wabwinodi
 Kwa ofuna kumva.
Ngakhale tingatope,
 Yesu atipatsa,
 Mpumulo ndi mphamvu zambiri;
 Tidzasangalala.
3. Abale ambirimбири,
 Otetezedwadi,
 Otumikira M'lungu,
 Padziko lapansi.
Tilipodi ambiri,
 Timalalikira,
 Timagwira ntchito ndi M'lungu,
 Pomutumikira.

1. Yehova ndi M'lungu wopanda tsankho.

Amasamalira mosakondera.

Amapatsa mvula,

Ngakhalenso dzuwa;

Amatisangalatsa mtima.

Osauka tikamawathandiza,

Mulungu wathu tidzamutsanzira.

Adzatidalitsa

tikamachitira,

Ena zinthu mokoma mtima.

2. Pothandiza ena sitingadziwe

Madalitso omwe tingalandire.

Angakhale anthu

achilendo ndithu,

Tiwapatse zosowa zawo.

Monga Lidiya wa m'nthawi yakale,

Akabwera kwathu tiwalandire.

M'lungu amadziwa

onse om'tsanzira,

Pochitira ena chifundo.

101 *Tizigwira Ntchito Mogwirizana* (Aefeso 4:3)

1. M'dziko logawikanali,
Tili m'gulu la Mulungu.
Timakhala mwamtendere,
N'zosangalatsadi.
Timaunyadira
Mgwirizanowu.
Palitu ntchito yambiri.
Yesu akutsogolera.
Ndiyetu tizimumvera,
N'kumagwirizana.
2. Popempherera umodzi,
Tizikondana kwambiri,
Chikondicho chidzakula,
Komanso mtendere.
Mtendere n'ngwabwino,
Utsitsimula.
Pamene tikukondana,
M'lungu adzatithandiza.
Kukhala ogwirizana,
Pomutumikira.

102 “Muthandize Ofookawo”

(Machitidwe 20:35)

1. Tonse timavutika,
Timafo’kanso.
Koma Mulungu wathu
Amatikonda.
Iye n’ngwachifundo;
Ndi wachikondinso.
Nafe tikonde ena,
Tiwathandize.
2. Atumiki a M’lungu,
Angafooke.
Tiziwalimbikitsa,
Ndi mawu athu.
Ndi anthu a M’lungu;
Amawalimbitsa.
Tiziwadera nkhawa,
Tiwatonthoze.
3. M’malo mowaweruza,
Tikumbukire
Kuti kukoma mtima
N’kolimbikitsa.
Tizichita khama,
Powalimbikitsa.
Tikamawathandiza,
Atonthozedwa.

103 *Abusa Ndi Mphatso za Amuna* (Aefeso 4:8)

1. Yehova amatithandiza,
Kudzera mwa 'busa.
Mwa chitsanzo chawo chabwino,
Amatiphunzitsa.

(KOLASI)

*M'lungu watipatsa amuna,
Omwe timadalira.
Amadera nkhawa tonsefe;
Ndiyetu tiwakonde.*

2. Abusawa ndi achikondi;
Amaleza mtima.
Tikapunthwa amathandiza,
Kutitu tichire.

(Kolasi)

3. Amatipatsa malangizo,
Tisasocheretu.
Tizisangalatsa Mulungu,
Ndi kum'tumikira.

(Kolasi)

104 ***Mzimu Woyera Ndi Mphatso
Yochokera kwa Mulungu***
(Luka 11:13)

1. Yehova 'Tate ndinu wamkulu,
 Kuposadi mitima yathu.
 Pamavuto mutithandizetu,
 Mzimu wanu utilimbikitse.
2. Ndife ochimwa, operewera;
 Nthawi zina timalakwitsa.
 Tikupempha mutipatse mzimu.
 Nthawi zonse utitsogolere.
3. Tikafooka, tikakhumudwa,
 Mzimu udzatilimbikitsa.
 M'tipatse mphamvu tisafooke;
 Tigawireni mzimu woyera.

105 “Mulungu Ndiye Chikondi”

(1 Yohane 4:7, 8)

1. Mulungu ndiye chikondi, wati:

‘Yendani nane.’

Tikonde M’lungu ndi anthu,

Tizichita zabwino.

Tidzasangalala ndithu;

Tidzapezanso moyo.

Tizisonyeza chikondi;

Ngati cha Yesu Khristu.

2. Tikakonda choonadi,

Tidzachita zabwino.

Tikalakwitsa n’kufo’ka;

M’lungu amatidzutsa.

Chikondi chilibe nsanje;

Ndipo chimapirira.

Choncho tizikonda ’nzathu;

Tidzadalitsidwadi.

3. Musalole kuti mkwiyo;

Ukutsogolereni.

Khulupirirani M’lungu;

Adzakuphunzitsani:

Kukonda M’lungu ndi anthu,

N’chikondi chenicheni.

Tizisonyeza anzathu

Chikondi cha Mulungu.

1. M'lungu tikupempha m'tipatse,
Makhalidwe anu onsewo.
Koma lofunika koposa
N'chikondi, mzimu 'matipatsa
Tingakhaletu ndi maluso,
Popanda chikondi n'ngachabe.
Tisonyezani chikondi,
M'zochita ndi muzolankhula.

2. Chikondi chimatithandiza
Kuti tikhaledi opatsa.
Sichimasunganso zifukwa,
Chimakhululukira ena.
Chikondi chimapiriranso,
Mavuto angakule bwanji.
Chikondi sichimagonjanso;
Chidzakhala mpaka muyaya.

107 Tizitsanzira Chikondi cha Mulungu

(1 Yohane 4:19)

1. Yehova M'lungu, n'chitsanzo chabwino
Inde cha chikondi.
Zochita zake, zimatithandiza
Kuti tizimutsanzira.
Anatipatsa, Mwana wake Yesu
Kuti tikhululukidwe zolakwa.
Monga umboni wa chikondi chake
M'lungu wathu, ndiye chikondi.
2. Tikatsanzira M'lungu tisonyeza
Chikondi choona,
Abale onse, tidzawathandiza
Mosasankha aliyense.
Tikonde M'lungu komanso anzathu,
Chimenechi ndi chikondi choona.
Tizikwirira zolakwa za ena,
Tidzasonyezadi chikondi.
3. Chikondi chathu chimatithandiza
Kumagwirizana.
Atate wathu akupempha kuti:
'Dzalaweni mgwirizano.'
Musangalale n'chikondi choona;
Mawu a M'lungu amatiyengatu.
Abale athu, amatikumbutsa,
Za chikondi cha M'lungu wathu.

108 Chikondi Chosatha cha Mulungu

(Yesaya 55:1-3)

1. M'lungu ndi chikondi.

Amatikonda kwambiri.

Anaperekatu Yesu

N'kuwombola anthu tonse,

Timayembekezeranso

Moyo wosangalatsadi.

(KOLASI)

Inu nonse a ludzu,

Dzamweni kwaulere.

Madzi opatsa moyo;

Mulungu n'chikondi.

2. M'lungu ndi chikondi.

Ntchito zake ndi umboni.

Wasonyezanso chikondi,

Popatsa Yesu Ufumu.

Ufumu wa Yesu pano.

Wayamba kulamulira.

(Kolasi)

3. M'lungu ndi chikondi.
Nafenso tichisonyeze.
Pothandiza 'nthu ofatsa,
Kusungatu malamulo.
Timamvera M'lungu wathu,
Tilalikira konseko.

(Kolasi)

*Tizikondana Kwambiri
Kuchokera Mumtima*
(1 Petulo 1:22)

1. Tikakhala ndi chikondi,
 Timasangalatsa M'lungu.
Mulungu ndiye chikondi,
 N'zosangalatsadi.
Nafe timakonda ena,
 Timapezadi mabwenzi.
Chikondi chenichenidi,
 Tizichisonyeza.

Ena akavutika,
 Tidzawathandiza mwamsanga.
Tidzakhalatu bwenzi,
 Lomwe limamvetsadi.

Yesu anatisonyeza,
 Chikondi cha M'lungu wathu,
Chimatikhudzadi mtima.
 Tizikonda anzathu,
Kuchokera mumtima.

**“Chimwemwe Chimene
Yehova Amapereka”**
(Nehemiya 8:10)

1. Zizindikiro zasonyeza kuti,
Ufumu wayandikira.
Chipulumutso chayandikiradi;
Tukulani mitu yanu!

(KOLASI)

Chimwemwe chochoka kwa Yehova.

Ndi malo achitetezo.

Imbani mofuula ndi chimwemwe,

Chifukwa cha chiyembekezo.

Chimwemwe chochoka kwa Yehova.

Ndi malo achitetezo.

Modzipereka tilambire M’lungu,

Mwachimwemwe tim’tumikira.

2. Inu nonse okondadi Yehova.
Muzimukhulupirira.
Imirirani ndipo fuulani;
Imbani mosangalala.

(Kolasi)

Tili Ndi Zifukwa Zambiri
Zokhalira Osangalala
(Mateyu 5:12)

1. Tili ndi zifukwa zambiri,
Zakuti tisangalale.
Anthu a mumitundu yonse
Akusangalala nafe.
Chisangalalo n'chachikulu,
Mawu a M'lungu tidziwa.
Timawaphunzira mwakhama;
Amatilimbikitsadi.
Zotisangalatsa n'zambiri,
Mumtimamu zikuyaka.
Tikakumana ndi mavuto,
Yehova amathandiza.

(KOLASI)

Amatisangalatsadi,
Yehova Mulungu wathu.
Ndi wabwinodi ndi ntchito zake,
N'zazikulu ndi zamphamvu.

2. Timasangalala kuona,
Kumwamba, nyanja ndi dziko.
Yehova analenga zonse,
Ife timayamikira.
Timachitiratu umboni,
Ndi kulengeza Ufumu.
Madalitso a Ufumuwo,
Tilengeza kulikonse.
Kusangalala kwamuyaya,
Kwayandikira tsopano.
Zimene anatilonjeza
Tidzasangalala nazo.

(Kolasi)

112 Yehova Ndi Mulungu Wamtendere

(Afilipi 4:9)

1. M'lungu wachikondi,
Mwalonjeza mtendere.
Mutipatse mzimu wanu;
Zipatso tisonyeze.
Chikhulupiriro,
Chimatithandizadi,
Kukhala mabwenzi anu;
Tili pamtenderedi.
2. Timamvetsa zinthu
Timaona kuwala.
Timatsogoleredwa
Mudziko lamdima ili.
Nthawi idzafika
Pomwe nkhondo zidzatha,
Dalitsani khama lathu
Tikhale amtendere.
3. Mulitu ndi gulu,
Kumwamba ndi padziko,
Lomwe ndi logwirizana
Lolengeza Ufumu.
Mu Ufumu wanu
Nkhondo mudzazithetsa.
Tidzakhala mwamtendere
Padziko kwamuyaya.

113 *Yehova Amatipatsa Mtendere* (Yohane 14:27)

1. Tamandani Yehova,
Wamtendereyo.
Nkhondo adzazithetsa,
Mwa Mwana wake.
Adzapambana nkhondo,
Yachilungamo.
Mtendere udzabwera,
Padziko lonse.
2. Tasiya kulankhula
Zokhumudwitsa.
Malupanga, mikondo,
Zonse tataya.
Tisungabe mtendere
Tikhululuke.
Monga nkhosa za Yesu,
Zamtenderedi.
3. Mtendere ndi umboni
wa madalitso.
Tasunga malamulo
a M'lungu wathu.
Timakonda mtendere,
Tiusonyeza
Mpaka M'paradaiso
Wamtendereyo.

1. Mbuye wathu Yehova,
Dzina lake ndi loyera.
Amafunitsitsatu
Kuliyeretsa dzinali.
Mumibadwo yambiri,
Iye ndi wopirira;
Amalezanso mtima,
Ndipo sakutopa.
Cholinga chake n’choti
Anthu adzapulumuke.
Adzapitirizabe
Kukhala woleza mtima.
2. Tikamaleza mtima
Tidzamvera M’lungu wathu.
Khalidweli n’labwino,
Timatha kupewa mkwiyo.
Timaona zabwino
Mwa ena nthawi zonse.
Limatithandizanso
Pa mavuto onse.
Makhalidwe enanso
Omwe n’zipatso zamzimu,
Adzatithandizadi
Kutsanzira M’lungu wathu.

*Tiziyamikira Kuleza
Mtima kwa Mulungu*
(2 Petulo 3:15)

1. Yehova wamphamvu zosatha,
Mumakondatu zabwino.
Zoipa n'zambiri m'dziko,
Mumadziwa n'zosautsa.
Simukuchedwa tikudziwa;
Posachedwa mudzazichotsa.

(KOLASI)

*Tiyembekeza mwachidwi,
Timatamanda dzina lanu.*

2. Zaka chikwi zilitu ngati,
Tsiku limodzi kwa inu.
Tsiku lanu lalikulu;
Layandikira kwambiri.
Anthu ochimwa akalapa,
Mumasangalala kwambiri.

(Kolasi)

Kukoma Mtima
N'kofunika Kwambiri
(Aefeso 4:32)

1. Tikukutamandani Yehova,
M'Malemba tapeza
Nzeru zanu zakuya ndi mphamvu,
Koma mumakoma mtima.
2. Yesu akuuza ovutika
Adzawathandiza.
Goli lake ndi lofewa ndithu,
Adzawatsitsimulatu.
3. Mulungu wathu ndi Mwana wake,
Ndi okoma mtima.
Nafe tikhale okoma mtima.
Tidzalimbikitsa ena.

1. Yehova, M'lungu wabwino,
Mumatidalitsadi.
Ndinu wokhulupirika,
Wabwino m'zinthu zonse.
Mumasonyeza chifundo,
Kwa anthu ochimwafe.
Tilambire inu nokha,
Tikutumikireni.
2. Taona ubwino wanu
Mwa atumiki anu;
Khalidwe lawo labwino
Ndi kulalikiranso.
Mwatipatsa mawu anu,
Ndi abusa abwino.
Mutipatse mzimu wanu,
Zabwino tizichita.
3. Tikachitirako ena
Zabwino m'tidalitse.
Tikhale okoma mtima
Kwa munthu aliyense.
M'mabanja ndi mumipingo,
Ndiponso kulikonse,
M'tithandize kuchitira
Anthu onse zabwino.

118 “*Tiwonjezereni Chikhulupiriro*”

(Luka 17:5)

1. Yehova ndifedi anthu ochimwa,
 Zoipa zimadzadza mumtima.
Pali tchimo lomwe limatikola—
 Kusowa kwa chikhulupiriro.

(KOLASI)

*M'tionjezere chikhulupiriro.
Tikupempha kwa inu Yehova.
Mwa chifundo chanu m'tionjezere,
Tikulemekezeni mu zonse.*

2. N'zosatheka kukusangalatsani.
 Ngati sitimakhulupirira.
Chikhulupiriro chimateteza.
 Ndipo chimatilimbitsa mtima.

(Kolasi)

*Tiyenera Kukhala Ndi
Chikhulupiriro*
(Aheberi 10:38, 39)

1. Kale Mulungu ankalankhula
Kudzera mwa aneneri.
Lero kudzera mwa Mwana wake,
Akuti, 'lapanitu.'

(KOLASI)

*Kodi chikhulupiriro
Chathu ndi cholimba ndithu?
Chikakhala chenicheni,
M'pamene tingadzapulumuke.*

2. Mosangalala timvera Yesu,
Tilalikira Ufumu.
Tilengezabe molimba mtima;
Anthu amve uthenga.

(Kolasi)

3. Talimbatu m'chikhulupiriro;
Sitidzabwerera m'mbuyo.
Tidziwa Yehova M'lungu wathu
Adzatipulumutsa.

(Kolasi)

120 *Tikhale Ofatsa Ngati Khristu*

(Mateyu 11:28-30)

1. Yesu anali wamkulu kwa anthu;
Koma sanadzikuze, sananyade.
Anali ndi udindo wapamwamba;
Komatu anali wodzichepetsa.
2. Kwa anthu omwe ali ndi mavuto,
Yesu akuti: 'Mundisenze onse.'
Akamafuna Ufumu choyamba.
Iye adzawachitira chifundo.
3. Yesu anati, 'tonse ndi abale.'
Timamumvera monga Mutu wathu.
Ofatsa ndi ofunika kwa M'lungu;
Adzalandira dziko lapansili.

121 *Timafunika Kukhala Odziletsa*

(Aroma 7:14-25)

1. Timakonda Yehova kwambiri;
Koma poti ndife anthu ochimwa.
Timafunika kudziletsa;
Mzimu udzatithandizadi.
2. Tsiku ndi tsiku timayesedwa,
Uchimowu umatisoheretsa.
Koma cho'nadi ndi champhamvu.
Yehova amatithandiza.
3. Tilemekeze dzina la M'lungu,
Muzochita ndiponso zoyankhula.
Cholinga chathu chizikhala:
Kukhala anthu odziletsa.

Khalani Olimba
Komanso Osasunthika
 (1 Akorinto 15:58)

1. Mitundu yavutika kwambiri.
 Anthu akuopa zam'tsogolo.
 Ife tilimbe tisasunthike,
 Potumikira M'lungu.

(KOLASI)

*Tiyenera kulimba;
 Tisiyane ndi dziko,
 Tikhale olimba,
 moyo tidzapeza.*

2. Misampha ndi yambiri m'dzikoli.
 Koma mwanzeru tingaipewe.
 Tikamadana n'zoipa zonse
 Sitidzasunthikadi.

(Kolasi)

3. Tizilambira Mulungu wathu.
 Tim'tumikire ndi mtima wonse.
 Tizilalikiradi mwachangu.
 Mapeto akubwera.

(Kolasi)

*Tizigonjera
Mulungu Mokhulupirika*
(1 Akorinto 14:33)

1. Tikamalengeza padziko lonse
Cho'nadi cha Ufumu wa Mulungu,
Tizitsatira malangizo ake
Tizichita zonse mogwirizana.

(KOLASI)

*Tizigonjera Mulungu wathu,
Mokhulupirika.
Amatikonda, amateteza,
Tikhulupirikedi.*

2. M'lungu watipatsa mzimu woyera,
Ndi kapolo azititsogolera.
Choncho tizisangalatsa Yehova,
Polalikira mokhulupirika.

(Kolasi)

124 *Tizikhulupirika Nthawi Zonse* (Salimo 18:25)

1. Tikhulupirike zedi,
Kwa M'lungu ndi kum'konda.
Malamulo ake onse,
Tifuna kuwadziwa.
Timapindula kwambiri,
Tikamamvera iye.
Ndi wokhulupirikadi,
Ndipo sitingam'siye.
2. Tikhulupirike zedi,
Kwa abale mumpingo.
Nthawi zonse pamavuto,
Amatisamalira.
Tiziwalemekezatu
Kuchokera mumtima.
Tiwamvere nthawi zonse,
Ndipo tisawasiye.
3. Tikhulupirike zedi
Tikamalangizidwa.
Ndi abale amumpingo,
Tifunika kumvera.
Ndipo Yehova Mulungu
Adzatalitsatu,
Tikakhulupirikadi,
Iye adzatichonda.

125 “Odala Ndi Anthu Achifundo” (Mateyu 5:7)

1. Yehova ndi wachifundo,
Amasonyeza chifundo.
Iye ndi wokoma mtima
Amatisamaliradi.
Ochimwa omwe alapa,
Adzamva pemphero lawo.
Amadziwa ndife fumbi,
Amatikomera mtima.
2. Tikachimwa n’kupemphera,
M’lungu amakhululuka,
Yesu anatiphunzitsa
Mmene tingapempherere:
‘Mukhululuke zolakwa,
Za ena takhululuka.’
Tisasungenso zifukwa,
Mtendere tidzaupeza.
3. Tikapatsa ena mphatso,
Tizisonyeza chifundo.
Tisamafune kutchuka,
Koma kungowathandiza.
M’lungu yemwe amaona,
Adzakubwezeranidi.
Achifundo n’ngachimwemwe,
M’lungu amawakondanso.

126

*Khalani Maso, Limbani
M'chikhulupiriro, Khalani Amphamvu*
(1 Akorinto 16:13)

1. Khala maso, upirire,
Ukhalebe wamphamvu.
Ukhale wolimba mtima,
Udzapambana ndithu.
Timvera lamulo la Yesu;
Tikhalebe kumbali yake.

(KOLASI)

*Khala maso, khala wamphamvu!
Limba mpaka mapeto!*

2. Khala maso, usagone,
Wokonzeka kumvera.
Uzimvera malangizo
Ochokera kwa Yesu.
Mvera malangizo a 'kulu,
Oteteza nkhosa, n'cho'nadi.

(Kolasi)

3. Khala maso, m'gwirizane
Poteteza uthenga.
Ngakhale uzitsutsidwa,
Uzilalikirabe.
Tamanda M'lungu mwachimwemwe.
Tsiku lake layandikira!

(Kolasi)

127 ***Mtundu wa Munthu Amene
Ndiyenera Kukhala***
(2 Petulo 3:11)

1. Ndipereke chani, kwa inu M'lungu
 Pokuthokozani, chifukwa cha moyo?
Mawu anuwa, amandiunikira;
 Ndithandizeni kuti ndidzifufuze.

(VESI LOKOMETSERA)

Ndalonjeza kutumikira inu,
 Mofunitsitsa ndi moyo wanga wonse.
Ndasankhatu ndekha kutumikira;
 Ndifuna kusangalatsa inu.

M'lungu n'thandizeni kudzifufuza,
 Ndikhaletu munthu amene mufuna.
Odalirika, mudzawasamalira;
 Nane ndifuna kusangalatsa inu.

1. Mawu a Mulungu wathu
Amalimbikitsa.
Zonse zomwe waphunzira
N'zolondola, n'zoona.
Limba m'chikhulupiriro,
Tsiku la Ya lafika.
Usaope mayesero;
Udzakhala wolimba.
2. Chikondi chako kwa M'lungu,
Chisachepe mphamvu.
Upirirebe ngakhale,
Mayesero akule.
Kaya akhale otani,
Usachitetu mantha.
Yehova Mulungu wako,
Adzakupulumutsa.

3. Yemwe angapirirebe
Adzapulumuka.
M' buku la moyo la M' lungu,
Adzalembedwamotu.
Lola kuti kupirira;
Kugwire ntchito yake.
Yehova adzachititsa;
Kuti usangalale.

1. Tiyenera

Kumapirira mayesero.

Paja Yesu

Anachitanso zimenezo.

Analimba mtima,

Podalira M'lungu.

(KOLASI)

Tikhale opirira

tizilalikira.

M'lungu amatikonda.

Adzatithandiza kupirira.

2. Tingakumane

Ndi mavuto ochuluka,

Komabe moyo

wosatha tidikirira.

Mtendere wosatha

tikulakalaka.

(Kolasi)

3. Sitichita

mantha kapena kukayika.

Titumikire

Mpaka tsiku lomaliza.

Tsiku la Yehova

lilidi pafupi.

(Kolasi)

1. Mwachikondi M'lungu
Anapereka Yesu
Kuti tikhululukidwe,
Ndi kuthetsanso imfa.
M'lungu amakhululuka,
Ngati ife talapa.
Nsembe ya dipo ya Yesu,
Imatithandizadi.
2. Tikamatsanzira
Chifundo cha Yehova
Pokhululukira ena,
Tidzakhululukidwa.
Tikhale ololerana,
Ndipo tisamadane;
Tizilemekeza ena,
Komanso kuwakonda.
3. Chifundo n'chabwino
Tonse tikhale nacho.
Sitidzasunga zifukwa,
Tikakhumudwitsidwa.
Tikatsanzira Yehova,
Yemwe ndi wachikondi,
Tidzakhululukirana;
Tidzafanana naye.

*“Chimene Mulungu
Wachimanga Pamodzi”*
(Mateyu 19:5, 6)

1. Mulungu ndi anthu,
Amva malonjezo.
Chingwe cholimba bwino,
Chamangidwa lero.

(KOLASI 1)

*Mwamuna walonjeza
Kukonda mkaziyu.
“Chomwe M’lungu wamanga,
Musalekanitse.”*

2. Onse afufuza
M’Mawu a Mulungu,
Kuti akwaniritse,
Zomwe alonjeza.

(KOLASI 2)

*Mkaziyu walonjeza
Kukonda mwamuna.
“Chomwe M’lungu wamanga,
Musalekanitse.”*

132 *Tsopano Ndife Thupi Limodzi* (Genesis 2:23, 24)

1. Fupa la mafupa anga,
Ndiwe mnofu wa mnofu wanga.
M'lungu wandipatsa mnzanga,
Iwe ndi wangadi.

Ndife thupi limodzidi;
Madalitso tizilandira.
Monga mwamuna ndi mkazi,
Pano ndife banja.

Titumikire M'lungu wathu.
Tsiku ndi tsiku,
Chikondi tikulitse.

Zimene talumbirazi.
Tizichita kwa moyo wonse.
Tizilemekeza M'lungu,
Ndipo ukhalebe wanga.

Lambirani Yehova
Mudakali Achinyamata
(Mlaliki 12:1)

1. Anyamata ndi atsikanafe,
Ndife ofunika kwa Mulungu.
Tikamam'tumikira mwakhama,
Azitidalitsa nthawi zonse.
2. Tikamalemekeza makolo
Timawasonyezatu chikondi.
Anthu ndi M'lungu amatikonda,
Tidzayandikira M'lungu wathu.
3. Tizikumbukira M'lungu wathu,
Tizikonda cho'nadi kwambiri.
Tikakhulupirika kwa M'lungu,
Tidzasangalatsadi Yehova.

**Ana Ndi Mphatso
Yochokera kwa Mulungu**
(Salimo 127:3-5)

1. Mwamuna 'kakhala bambo
Mkazinso akakhala ndi mwana,
Ayenera kukumbukira,
Mwanayo si wawo okha.
Ndi mphatso yochoka kwa M'lungu;
Amapatsa chikondi ndi moyo.
Amapereka malangizo
Othandizadi kwa makolo.

(KOLASI)

*Mphatsoyi ndi yopatulika;
Ndipo muisamalire.
M'phunzitseni mwana cho'nadi;
Ndipo mudzamuthandiza.*

2. Mawu onse a Mulungu—
Azikhalatu pamtima panu.
Muuzanso ana anu,
Uwu ndi udindo wanu.
Muziwaphunzitsa poyenda,
Podzuka ndi pa nthawi yopuma.
Akamakula saiwala,
Adzalandira madalitso.

(Kolasi)

135 ***Yehova Akutipempha Kuti:***
“Mwana Wanga, Khala Wanzeru”
(Miyambo 27:11)

1. Mwana wanga undipatse
 mtima wako.
 Yemwe akunditonza
 aone yekha.
Ukudziperekadi
 mofunitsitsa;
Anthu adziwe
 kuti umandikonda.

(KOLASI)

*Mwana wanga wokonedwawe,
Khalatu wanzeru chonde.
Kutitu unditumikire,
Inde mwakufuna kwako.*

2. Uzinditumikira
 mosangalala,
 Ngakhale ukapunthwa,
 ndidzakudzutsa.
Wina ngakhale
 angakukhumudwitse,
Usadere nkhawa
 ndidzakhala nawe.

(Kolasi)

136 Yehova “Akufupe Mokwanira”

(Rute 2:12)

1. Yehova amadziwa anthu onse
Omwe amam'tumikira.
Amadziwa bwino mavuto awo,
Zomwe amadzimananso.
Ngati mwasiya abale ndi nyumba,
Zonse M'lungu akudziwa.
Amatipatsa 'bale auzimu,
Moyo m'dziko latsopano.

(KOLASI)

*Yehova akupatseni mphoto.
Akufupeninsu mokwanira.
Mubisale m'mapiko ake.
N'ngokhulupirika, sanganametu.*

2. Nthawi zina timakhala ndi nkhawa
Poganizira moyowu.
Mwinanso kupeza zofunikira
Kungakhaletu kovuta.
M'lungu amadziwa zomwe m'mafuna,
Amamvanso mapemphero.
Mawu, mzimu wake ndi mabwenzinso
Adzakulimbikitsani.

(Kolasi)

137 Akazi Achikhristu Okhulupirika

(Aroma 16:2)

1. Sara, Esitere, Rute, ndi ena—
Onsewa 'nali akazi abwino,
Anali odzipereka kwa M'lungu.
Timawadziwa ndi mayina awo.
Panali ena sanatchulidwe,
Iwotu Yehova ankawakondanso.
2. Akaziwatu amatikumbutsa
Makhalidwe omwe tifunikira.
Monga ubwino ndi kulimba mtima.
Ndi zitsanzo zotilimbikitsadi.
Alongo a masiku anonso,
Khalani zitsanzo kwa ena tonsefe.
3. Achemwali, amayi, amasiye
Mumachita khama pogwira ntchito
Mumagonjera, mumadzichepetsa.
Musaope Mulungu ali nanu.
Ndipo iye akulimbitseni,
Musafooketu, mudzadalitsidwa.

138 *Imvi Ndi Chisoti cha Ulemerero* (Miyambo 16:31)

1. Pano tili ndi anthu
Achikulire.
Akukondabe M'lungu;
Sanamusiyе.
Enatu umasiye
Ukuwawawa
Tate, atonthozeni,
Alimbitseni.

(KOLASI)

Mumakumbukira

Zochita zawo.

Tate auzeni:

“Mwachita bwino!”

2. Imvi za olungama
Ndi zokongola.
Zimasangalatsadi
Tate Yehova.
Ife tikumbukire
Pa nthawi ina.
Pa unyamata wawo
Ankayesetsa.

(Kolasi)

139

*Yerekezerani Kuti
Muli M'dziko Latsopano*
(Chivumbulutso 21:1-5)

1. Yerekeza ukuona;

Iwe ndi 'ne m'dziko latsopano.

Ona mmene udzamvere

Kukhala m'dziko lamtendere.

Oipa onse achoka.

M'lungu wathu sadzalephera.

Kusintha zonse padziko lapansi,

Tidzamuimbira nyimbo

tikumati:

(KOLASI)

“Tikuthokoza mwachita bwino.

Zonse zakhaladi zatsopano.

Tikuimba nyimbo mwachisangalalo

Ndinudi woyenera ulemerero.”

2. Taganizira m'tsogolo;
Iwe ndi 'ne m'dziko latsopano.
Sitidzamva ndi kuona
Zinthu zotichititsa mantha.
Mmene analonjezera;
Zinthu zonse zachitikadi.
Tsopano aku'kitsanso akufa;
Iwo ndi ife
tidzamuyamikira:

(Kolasi)

140 *Tidzapeza Moyo Wosatha* (Yohane 3:16)

1. Onani m'maganizo,
Anthuwo pamtendere.
Chisoninso chathadi!
Kulira kwathanso.

(KOLASI)

*Imbani mokondwa!
Ngakhale inunso.
Patsikulo mudzati,
“Moyo wosathadi!”*

2. Anthu sadzakalamba.
M'lungu adzawakonda.
Mavutowa adzatha,
Anthu sadzalira.

(Kolasi)

3. Tidzasangalalatu
Poimbira Mulungu.
Tizidzalemekeza
Yehova Mulungu.

(Kolasi)

1. Makanda onse, ndiponso mvula,
Mbewu komanso kuwala kwa dzuwa—
Mulungu ndiye amatipatsa
mphatsozi ndipo zimatithandizadi.

(KOLASI)

*Tingachite chani ndi mphatso iyi?
Tikonde Mulungu yemwe anatipatsa.
Sitingaipeze mphatsoyi patokha,
Mphatso yake ndiyo moyo wodabwitsa.*

2. Ena 'ngasiye kulimba mtima,
N'kunena kuti: 'Kuli bwino kufa.'
Koma ifeyo sitili choncho.
Timayamikira kukhala ndi moyo.

(KOLASI)

*Tingachite chani ndi mphatso iyi?
Tikonde anzathu amene tili nawo.
Sitingaipeze mphatsoyi patokha,
Mphatso yake ndiyo moyo wodabwitsa.*

Tigwire Mwamphamvu Chiyembekezo Chathu

(Aheberi 6:18, 19)

1. Anthu akhala akuyenda mumdima.
Ndipo sanapindule kalikonse.
Zadziwika kuti anthu ochimwa;
Kuvutika sangakuthetse.

(KOLASI)

*Tiyeni tiimbe mokondwera!
Poti Ufumu wa M'lungu wabwera.
Yesu adzachotsadi zoipa;
Chiyembekezochi n'chodalirika.*

2. Uthenga womwe ukumveka ndi woti;
“Tsiku la Mulungu layandikira.”
Anthu sadzakhalanso ndi chisoni.
M'lungu wathu timuimbira.

(Kolasi)

143

*Pitirizani Kugwira Ntchito,
Kukhala Maso ndi Kudikira*
(Aroma 8:20-25)

1. Nthawi ya Mulungu wathu,
Yayandikira kwambiri—
Kutitu alamulire
Umboni waoneka.

(KOLASI)

*Pitirizani kukhala maso,
Kuti mudzapeze moyo,
Womwe M'lungu wakonza.*

2. M'lungu anaika nthawi;
Yoti Yesu agonjetse,
Adani ake onsewa.
Iye adzapambana.

(Kolasi)

3. Mavuto m'chilengedwechi,
Akuchuluka kwambiri.
Tiyembekeze Yehova,
Adzatipulumutsa.

(Kolasi)

1. Pomwe osaona 'kuwona

Ovutika kumva akumva,
Ana adzaimbanso nyimbo,
Mtendere padziko lonse,
Omwe anafa adzauka,
Uchimo, mavuto zathanso,

(KOLASI)

*Mudzaona zinthu zonsezi,
M'kayang'anabe pamphoto.*

2. Mimbulu idzadya ndi nkhosa,

Zilombo zoopsa ndi ng'ombe,
Mwana adzazitsogolera,
Zidzamvera mawu ake.
Pamene misozi idzatha,
Mantha ndi zowawa zathanso,

(Kolasi)

145 *Mulungu Watilonjeza Paradaiso* (Luka 23:43)

1. M'lungu wathu watilonjeza,
Paradaiso mwa Khristuyo,
Adzachotsa uchimo, imfa,
Misozi ndi zopweteka.

(KOLASI)

*Paradaiso adzafika.
Ndipo tikhulupirire.
Khristu adzakwaniritsa,
Chifuniro cha Mulungu.*

2. Cholinga cha Mulungu n'choti,
Yesu aukitse anthu.
Paja Yesu analonjeza,
'Udzakhala m'Paradaiso.'

(Kolasi)

3. Yesu Mfumu, analonjeza,
Paradaiso padzikoli.
Tithokoze Atate wathu,
Kuchokera mumtimamu.

(Kolasi)

146 “Ndikupanga Zinthu Zonse Kukhala Zatsopano” (Chivumbulutso 21:1-5)

1. “Zizindikiro” zikusonyezatu.

Kuti Yesu akulamulira.

Wachotsatu Satana kumwamba,

Posachedwa am’chotsa padziko.

(KOLASI)

Sangalalani chifukwa,

M’lungu alitu ndi anthu.

Iye adzachotsatu imfayi,

Chisoni ndiponso zowawazi.

‘Zonse zidzakhala zatsopano.’

Mawuwa ndi oona.

2. Anthu aone Yerusalemuyo,

Mkwatibwi wa Mwana wa Nkhosayo,

Atavala mochititsa chidwi,

Yehova ndiye kuwala kwake.

(Kolasi)

3. Mzindawu udzasangalatsa anthu.

Uzidzakhala wosatsekedwa.

Anthu adzayendatu mowala;

Atumikinu muziwalabe.

(Kolasi)

Mulungu Watilonjeza Moyo Wosatha

(Salimo 37:29)

1. Mulungu watilonjeza.
Moyo womwe sudzatha.
'Ofatsa 'dzasangalala.'
Zidzachitikadi.

(KOLASI)

*Tidzakhala ndithu,
Ndi moyo wosatha.
M'lungu walonjeza.
Zidzachitika.*

2. Paradaiso akubwera;
Anthu adzamasuka.
Kudzakhaladi mtendere,
Wochoka kwa M'lungu.

(Kolasi)

3. Akufawo adzauka,
Chisoninso chidzatha.
Mulungu adzapukuta,
Misozi ya anthu.

(Kolasi)

148 Yehova Amapereka Populumukira

(2 Samueli 22:1-8)

1. Yehova ndinudi Mulungu wamoyo;
M'chilengedwe chonse
Mphamvu zaoneka.
Palibe M'lungu wina angachite
—zimene
Inu mumachita.

(KOLASI)

*Yehova ndiye pothawira pathu.
Tidzaonadi kuti iye ndi Thanthwe.
Tilengeze molimba mtima
mphamvu zake.
Yehova m'pothawira pathu,
tim'tamande.*

2. Zingwe za imfa zingandizungulire,
ndidalira inu,
“Mundipatse mphamvu,
mundilimbitse mtima.”
Mumve kulira kwanga
“Ndibiseni M'lungu.”

(Kolasi)

3. Mudzagunda ngati
mabingu kumwamba.
Adzanjenjemera;
Adani anuwo.
Mudzakhala chimene mukufuna
kukhala
Onse adzaona.

(Kolasi)

***Tiimbire Yehova
Chifukwa Wapambana***
(Ekisodo 15:1)

1. Timuimbire Yehova M'lungu wokwezeka.
Waponyera m'nyanja Aigup'to onyada.
Titamande Ya;
Palibenso Mulungu wina.
Yehova ndi dzina lake;
ndi wopambana.

(KOLASI)

*Yehova ndinu wokwezeka,
Simunasinthe ndinudi Mfumu,
Posachedwa 'dani mugonjetsa
N'kuyeretsa dzina lanu.*

2. Mitundu yonse ikutsutsana ndi Yehova.
Ichita manyazi,
Ngakhale ndi yamphamvu.
Pachiweruzo;
Singathawetu Amagedo.
Idzadziwa kuti
Yehova ndi Mulungu.

(Kolasi)

150

*Bwerani kwa Mulungu
Kuti Mupulumuke
(Zefaniya 2:3)*

1. Mitundu ya anthu,
Ikutsutsabe Yesu.
Nthawi yoti alamule
Yatha watero M'lungu.
Ufumu wa M'lungu;
Ukulamuliratu.
Yesu adzachotsa adani.
Mwamsanga adzathadi.

(KOLASI)

*Bweranitu kwa Yehova,
Kuti mudzapulumuke.
Musakayike,
Muzimumvera,
Mukhale kumbali yake.
Adzakupulumutsani
Ndi mphamvu zake.*

2. Anthu akusankha,
Kumvetsera uthenga.
Timalalikira onse
Koma ena 'makana.
Mavuto akagwa,
Tisakhale ndi mantha.
Yehova 'dzatisamalira;
Tikam'khulupirira.

(Kolasi)

1. Moyo wathu sumachedwa kutha,
Timafadi mwamsanga.
Mukanthawi kocheпа kwambiri,
Timayamba kulira.
Kodi akufa angadzukenso?
M'lungu akulonjeza:

(KOLASI)

*Iye adzawaitana;
Akufa adzayankha.
Ntchito ya manja ake.
Adzailakalaka.
Inu musakayikire,
M'lungu adzatidzutsa.
Tidzakhala kosatha,
Mongadi anthu ake.*

2. Anthu a M'lungu akamwalira,
Iye sawaiwala.
Omwe amawakumbukiratu,
Iye adzawadzutsa.
Ndipo tonse tidzasangalala
Ndi moyo m'paradaiso.

(Kolasi)